


MAFUNSO NDI MAYANKHO

AHEBRI, GAWO III

 ...kukhala ndiri pano usikuuno kachiwiri ku Kachisi, kudzayembekezera chiyanjano chodabwitsa ichi ndi kupembedza pozungulira Mawu a Mulungu omwe anaperekedwa kwa ife mwaulere. Ndipo ife tiri...kukonda kukhala ogawana nawo dalitso limeneli.

⁵⁵⁴ Ndipo ine ndikungodalira kuti Mulungu atidalitsa ife usikuuno monga Iye anachitira mmawa uno, ndi uthenga wa mmawa. Ndipo ine ndinali kungoyankhula kwa woyandikana naye wanga, Akazi a Wood, kanthawi kapitako, ndipo ife tinali kukambirana izo, ndipo Bambo Wood ndi iwo. Ndipo ine ndikukhulupirira uja unali ulaliki wopambanitsitsa wa M'bale Neville mwa wonse wabwino womwe iye analalikirapo, uja unali umodzi womwe unali wabwinoko kwa ine kuposa wina uliwonse womwe anayamba walalikira panobe. Ine ndithudi ndinayamikira ndi kuyamikira ulaliki wodabwitsa uja. Ndipo iwo unandipatsa ine chilimbikitso, ndipo iwo unandidulira ine pansi. Kotero i—ine ndimakonda kuvomereza zoono, inu mukudziwa. Chotero, za magawo akulimbamtima, inu mukudziwa, kukhala wolimbamtima, ndi momwe... Davide analiri uko, ndi momwe kuti iye... Pamene anali mu kuyesedwa kwakukulu kuja, mmalo monena kuti “Chabwino, ine ndipita ndikachite izi, Ambuye, Inu mungondithandiza ine,” iye anadikirira, napita ndi kukawafunsa Ambuye zoti angachite. Iye anabweretsa uko chapachifuwa, inu mukudziwa, ndipo anati, “Tsopano tiyeni tiime ndi kumufunsa Mulungu, ‘Kodi ife tichite chiani mu vuto ili?’” O, izo zinali zolemera kwenikweni. Izo zinali ndi mavitamini ochuluka kuposa masitolo onse azamankhwala omwe ali nawo mu dzikoli. Inde, bwana, izo zimakuchitira iwe ubwino kwenikweni.

⁵⁵⁵ Tsopano, usikuuno, i—ife sitikulinga kuti tikhale osatinso motalika kupitirira pakati pa usiku, ngati ife tingathe, pa mafunso awa. Chotero ife—ife tikuti tilowe kumene mu iwo, pomwe pano. Ndi kutsirizitsa kwa mafunso awa, ndipo nthawi iliyonse ine ndikayamba kuti ndiwatsirize iwo... (tsopano, Mlongo Hattie, ine sindimatanthauza izo, inu mukudziwa izo. I—ine ndinali kungonena izo, mwaona; ndi, chabwino). Koma ine ndiri nawo ena olimba kwenikweni pano ochokera kwa mtumiki, ndipo iwo ndi ovuta kwenikweni kuti uwayankhe. Inu mukudziwa, alaliki awo, iwo amazipotozera izo mozungulira kudutsa mu Baibulo ndi kuyesa kuti apeze yankho lawo lawo iwo asanakufunse iwe, inu mukuona. Ndiyeno... ndipo izi ziri

kujambulidwa pa tepi, zipita uko ku Georgia kwa mtumiki mzanga yemwe ali ndi mafunso eyiti opambana a Baibulo pano omwe ali okuya kwambiri mbiri.

⁵⁵⁶ Ndipo tsopano, sabata ikubwerayi, musati muiwale ndi kutipempherera ife.

⁵⁵⁷ Ndipo mkazi wanga ali bwino mochuluka; iye akuimirira tsopano, ndipo iye anathandizira kuphika, lero. Abwenzi athu okondedwa ochokera ku Canada, M'bale, Mlongo Sothmann, ali kuno kudzatichezera ife, ndipo ife ndithudi tikuyamikira kutichezera kwawo. Ndipo mkazi wanga, podziwa kuti iwo amabwera, bwanji, iye anali woti akhale akuimapo chotero kuti iye akhoze kukhala ndi zina zowasangalatsa ndi chiyanjano nao anthu okondedwa Achikristu awa. Ndife okondwa kukhala naye M'bale Freddie usikuuno, ndipo iye anakhala ndi... Iye anali kuno mmawa uwu, koma ine ndikukhulupirira iye anakhala ndi... ayi, uko nkulondola, iye ali ndi Meda, kuti akhale ngati ali ndi iye pamene ife timabwera kuno; chifukwa ine ndikudziwa izi zikhala mochedwerapo pang'ono usikuuno, ndi mgonero ndi kutsukana mapazi. Chotero ndife okondwa kukhala nawo iwo ndi alendo omwe ali nafe.

⁵⁵⁸ Tsopano, ife tisanayambe kuyesera kuti tichitepo zoyankha mafunso... Ndipo ingokumbukirani kuti i—ine ndikhoza kukhala ndikulakwitsa, inu mukuona, i—ine sindimadzinenera kuti ndine wolondola pa chirichonse chimene ine ndimachita. I—ine ndimayesera kuti ndizikhala wolondola, koma mwinamwake i—ine ndikulakwitsa. N—ndipo ngati ine ndikulakwitsa, ndiye inu mungondikhululukira ine; ndipo ine ndipemphera Mulungu kuti atero, nayenso, chifukwa ine sindikutanthauza kuti ndikhale ndikulakwitsa. Ine sindikuyesera kuti ndiwayankhe iwo kungoti—... kapena momwe ine basi... mwa kukondera, ine ndimawayankha iwo mwa kukhoza kwa kudziwa kwanga kopambana, mwaona. Ndipo ngati ine ndingasowe kuti ndisithe malingaliro anga pa funso la Baibulo, ine ndikuganiza basi ndicho chinthu choti nkuchichita. Ife tiyenera kuti tizisintha, nthawi iliyonse, pamene Mawu a Mulungu ayankhula; chifukwa ndi Mawu a Mulungu.

⁵⁵⁹ Ndipo tsopano, ine ndikuganiza ife tikuti tipempherenso odwala usikuuno, mwa chizolowezi. Ndipo nthawizina iwe umangodabwa; iwe umatenga monga gulu laling'ono longa ili, locheperapo, o, Kachisi wamng'onoyu kuno, ndipo nthawizina iwe sumawona zotsatira zomwe iwe ukanafuna kuti uziziwona. Koma chinthu, chimene iwe ukuchita, iwe ukungokoka kuchokera kwa pafupi anthu thuu handiredi. Ndipo mu umodzi wa misonkhano yaikulu, mwinamwake iwe ukukokera kulikonse kuchokera kwa firii mpaka teni sauzande, inu mukuona, n—ndi mwina oposerapo. Kotero ndiyo njira yake, yomwe iwe umafikira powona unyinj wochuluka. Koma usikuuno, ine

ndakhala ndikungoyankha...Chifukwa foni yathu imalira maminiti angapo aliwonse kudutsa mu tsiku ndi gawo la usiku.

560 Kodi awa ndi Akazi a Reiser akhala apawa, omwe ine ndikuwayang'anawa? Baibulo lanu, mlongo, Mlongo Wood ali nalo kumbuyo uko. Ine ndinakubwereterani ilo mmawa uno kudzakupatsani inu, ndipo i—ine sindinathe kulipereka ilo kwa inu. Ndipo i—ine sindinakuwoneni inu mmawa uno, ndipo Akazi a Wood ali nalo.

561 Chotero poyankha foni ndikupeza z—zinthu zazikulu zomwe zakhala zitachitidwa. Dona anandiimbira ine, iye anati, “M'bale Branham, ine ndinali mu msonkhano *wakuti-n-wakuti* ndipo ine ndinali ndikuvutika ndi vuto *lakuti-n-lakuti* motalika chotero. Ndipo, inu mukudziwa, inu munangoyankhula kumbuyo kuja, ndipo basi...” Anati, “Ine ndinali pafupi kuti ndikomoke pamene Iwo unangobweretsanso apo moyo wammbuyo.” Ndipo anati, “Ndipo ine sindinadwalenso kuyambira apo.”

562 Ndipo dona anadzalowa umo ndipo anati...Ine ndikukhulupirira iye ali pano usikuuno, kapena iye amati ayendetse kuchokera ku Bedford, ine ndikukhulupirira, kapena kwinakwake kumtunda uko. Mwana wawo anali muno kuno, ine ndikukhulupirira, yemwe anali ndi vuto la mtima, mu mawonekedwe oipa chotero awo. Ndipo iye anali atakhala muno mu msonkhano, n—ndipo Ambuye anasunthira ndipo anamukhudza...ananena kwa mnyamatayo za vuto lake, ndipo iye sankatha nkomwe kudzutsa nkono wake, ndi vuto la mtima, ndipo nkono wake wonse utachita dzanzi, ndi mtima wake monga chonchi. Ndipo mwamsanga iye anakalowa mu galimoto momwe ndipo anayendetsa wa kwao, sanakhale akuvutitsidwapo ndi izo kuyambira apo. Kodi dona ameneyo wafika kuno wochokera ku Bedford? Kodi inu muli pano, dona? N—ndi uyo apo, mmbuyomo. Inde, anangondiimbira ine, kanthawi kapitako.

563 Ndiye pali dona yemwe anandiimbira ine kuchokera uko ku Evansville. Ndipo iye sakanakhoza kudzafika kuno chifukwa iye ali kutali kwambiri, samadziwa kuti ife tikhala ndi msonkhano usikuuno wa machiritso. Ndipo iye anati, “M'bale Branham, ine ndinali nditakhala mu msonkhano waku Evansville,” ndipo anati, “inu munayang'ana mmbuyo pa osonkhana ndipo munati...munandiuza ine yemwe ine ndinali, ndi zomwe ine ndinali nditazichita, ndi zomwe ine ndinali nditavutika nazo, ndi zina zotero monga choncho.” Ndipo iye anati, “Ine ndinali ndi chikhalidwe cha mphumu icho, ndipo ine ndinkachita kumawotcha mankhwala a mphumu ndi chirichonse mu chipinda kuyambira ndiri msungwana wamng'ono.” Anati, “Izi zakhala ziri zaka ziwiri zitapitapo, ndipo ine sindinayambe ndakhalapo ndi dontho limodzi la izo kuchokera apo.” Mukuona?

564 Ndipo basi chifukwa cha iwo omwe ali pano usikuuno, omwe sanali pano mmawawu kuti asangalale ndi umboni; ine ndinali ku sitolo ya teni-cent uko, ndikugula chidole, dzulo. Tsopano, icho sichinali cha mwiniwanga, mwaona. Icho chinali cha msungwana wanga wamng'ono, Rebekah, apo. N—ndipo Sarah anali kupita ku chinachake, chimzake, lero. Ena a amzake aku sukulu anali ndi mtundu wina wa kubwera palimodzi, pa tsiku lobadwa kapena chinachake, ndipo iye anali kumutengera iye mphatso yaing'ono; ndipo ine ndinali kugula kachidole kakang'ono ka mwana, kotalika chonchi. Ndipo uko kunali dona anayenda nabwera apo, anati, “Inu mukundikumbukira ine?”

565 Ndipo ine ndinati, “Ine sindikukhulupirira ine ndiri.”

566 Ndipo nkufika pozindikira kuti, uyo anali wapachibale kwa M'bale Neville kuno, yemwe pafupi. . . pamene ine ndinali paulendo wanga waku Sweden, iwo. . . Iye anabwera muno, anali ndi mnyamata wamng'ono mu chikuku, monga ngati Edith wamng'onoyo apo, ndipo munthu wamng'onoyo anali ndi khansa, chithupsya chokupsya pa ubongo. Ndipo mutu wake waung'ono atauweramitsa pansi, ndipo iye. . . ndipo madokotala anali atamupatsa iye masabata atatu okha kuti akhale moyo. Iwo anali atachichotsa icho apo ndipo atachipima icho, ndi kuwona ngati icho chinali. . . chomwe icho chinali, ndi kungomupatsa iye masabata atatu oti akhale moyo. Ndipo iwo anachita kumuyendetsa iye apo mu chikuku, ndiyeno anamuika iye pa machira pamene iye ankapita mu chipinda kuti akamupime iye, ndiyeno nkumubweretsanso iye kuno. Ndipo ndinapita nkukamupempherera mnyamata wamng'ono uyo, ndi kuwafunsa Ambuye kuti amuchize iye. Ndipo tsiku lotsatira lomwe, pamene iwo anamutengera iye uko, anati, “Ine sindikuchifuna chikuku icho.”

567 Analowa mu galimoto ndipo anayendetsa kupita uko, ndipo adokotala anatambasula machira, anati, “Ine sindikuwafuna machira awo.”

568 Anathamanga nakwera umo nkukakhala pansi, adokotala anamupima iye, anati, “Chabwino,” anati, “mmalo mwa masabata atatu, ine ndikuti ndikupatse iwe zaka handiredi ndi eyiti ukhale moyo.”

569 Ndipo, dzulo, amake anakomana nane. Ndipo iwo akhoza kukhala ali pano, mwa zonse zomwe ine ndikuzidziwa, usikuuno. Ndipo mnyamata wamng'onoyo anali ali kunja akusewera mpira, bambo wamng'ono tsopano. Chithupsya, khansa pa ubongo, ndipo izo ziri kungosonyeza. . .

570 O, zinthu zikwi, mwaona, Mulungu sangakhoze kulephera. I—Iye sangakhoze kulephera basi.

571 M'bale John, kodi diso lanu liri bwinoko, m'bale? Iye anali ndi ngozi, iye anali akukhomerera msomali ndipo iwo unamubaya iye mu diso. Ndipo ife tonse tinali kumupempherera

M'bale John O'Bannon, m'bale wathu wa ku Louisville yemwe anachita ngozi ndi msomali umene unamubaya iye mu diso.

⁵⁷² Tsopano, mafunso awa ali—mwa kuya kwa mtima wa winawake; zomwe iwo anawerenga podutsa mu Lemba ndipo anapezamo zinthu izi, ndipo iwo sali...mwina sangakhoze kudzikhutitsa okha, chotero iwo awapereka iwo kuno kuti ife tiyesere kuwayankha. Ndipo inu mukuona mpanipani omwe izo zikutiikamo ife; chifukwa, zomwe iwe unganene, iwo angatsamire kwa izo. Chotero iwe uyenera kumakhala motsimikiza kuti iwe ukulondola, ndipo ine m...motsimikiza basi momwe iwe ungakhale uli. Chotero ndiye, chintha choti titsimikize kuti ife tikulondola, tiyeni ife tingowufunsa Mzimu Woyera tsopano kuti utanthauzire izi kwa ife, pamene ife tikuweramitsa mutu wathu.

⁵⁷³ Tsopano, Atate Akumwamba, o, mwayi wake womwe uli kunena “Atate” kwa Mlengi wamkulu wa miyamba ndi dziko lapansi. Ndipo ife tikungokupemphani inu kuti muwatenge mafunso awa mwa kusamalira Kwanu Komwe tsopano. Iwo anaperekedwa pano ndi kuya kwa kuwonamtima. Mulungu, mulole izo zibwere kuchokera mmitima mwathu, mwa kuya kwambiri kwa kuwonamtima, kuti tiwayankhe iwo mwa kupambana komwe ife tikudziwira kutero; perekani izi.

⁵⁷⁴ Ndipo mulole zifundo Zanu zikhale pa aliyense. Ndipo mulole chinachake kuti chinenedwe pano usikuuno chomwe chiti chingomuthandiza aliyense yemwe ali pano. Ndipo pamene ife tizichoka, kutatha kupempherera odwala ndi kutenga kwa mgonero ndi zina zotero, mulole ife tinene monga aja omwe ankachokera ku Emau, “Kodi mitima yathu siimatentha mkati mwathu pamene iye anali kuyankhula kwa ife mnjira yonseyo?” Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

⁵⁷⁵ Tsopano, monga ine ndanena nthawi zambiri, kuti i—izi apa ndi z—zopambana za kulingalira kwanga pa izo, ndiyeno nthawizina zimautsa zokambirana pang'ono. Loyamba lake pano, ine ndikuwona ndi chinachake chomwe ine ndinanenepo kale, lomwe laperekedwanso kachiwiri. Ine sindi...ndikufuna kuti ndiliwerenge ilo tsopano, ngati inu mungathe.

65. Pamene Adamu ndi Eva anali ndi ana awo mu Edeni, kodi uko kunali anthu ena padziko lapansi pa nthawi iyi? Mu Genesis mutu wa 5 ndi ndime ya 16, Kaini anakakhala mu dziko la Nodi ndipo anamudziwa mkazi wake.

⁵⁷⁶ Tsopano, ilo—ndi funso lodabwitsa. Tsopano, ife timaphunzitsidwa mu Baibulo...Ndipo nthawizambiri izi...nthawizina ife mosasamala...ine ndinkakonda kuikapo kachidutswa kakang'ono ka pepala, ndi kuti, “Funsani. Ndiyankha funso lirilonse la Baibulo.”

⁵⁷⁷ Ndipo winawake anati, “Chabwino, n'ndani anali mkazake wa Kaini?”

578 O, ine ndinkachita nthabwala pang'ono pa ilo kapena chinachake, ine ndinkati, “O, uyo anali mwana wamkazi wa apongozi ake aakazi,” kapena chinachake monga choncho, inu mukudziwa, k—kapena “Iye anali Akazi a Kaini.” Koma izo sizimayankha funsolo. Pali . . .

579 Uko Kaini anali ndi mkazi, chifukwa Baibulo limati iye anali naye. Ndipo ngati Kaini anali ndi mkazi, iye anayenera kuti akamutenge iye kwina kwake. Ndipo izi zikanagwirizana limodzi kumene ndi izi apa:

Kodi kunali anthu ena pa dziko lapansi pamene Adamu ndi Eva anali ndi ana awo mmunda wa Edeni?

580 Tsopano, ngati inu mungazindikire, mu Baibulo sikawirikawiri kuti ankalemba za mkazi akakhala atabadwa. Izo nthawizonse anali mwana wamwamuna ndi yemwe ankamulemba mu Baibulo, osati mkazi. Sikawirikawiri kuti zimatchulidwa konse za kubadwa kwa mwana wamkazi, mu Baibulo. Kapena, moona, ine sindikudziwa momwe ine ndingakumbukirire za mmodzi molunjika apa pakalipano, mu malingaliro, pamene anayamba alembapo za kubadwa kwa mwanayo; limati, “Iwo anabala ana aamuna ndi aakazi.”

581 Tsopano, Baibulo limangopereka umboni wa ana atatu omwe anabadwa kwa Adamu ndi Eva, ndipo amenewo anali Kaini, Abele, ndi Seti. Tsopano, ngati atatu onse awo ali amuna, ngati kunalibe aakazi aliwonse atabadwa, ndiyeno pamene wamkazi yekha (Eva) anafa, mtundu wa anthu ukanasiya kukhalapo apo pomwe, chifukwa sipakanakhala pali njira iliyonse kuti iwo—akhale ndi alionse. . . mtundu wa anthu kuti upitirire, chifukwa sipakanakhala pali akazi otsalirapo. Eva akanakhala ali mmodzi yekha. Koma, inu mukuona, iwo samalemba—kubadwa kwa ana aakazi, mu Baibulo, choncho chotero iwo anayenera kukhala nawo atsikana chimodzimidzi monga anyamata.

582 Tsopano, mlembi wakale, mmodzi wa alembi amakezana omwe ife tiri nawo, Josephus, amanena kuti iwo anali ndi ana sevente, ndi Adamu ndi Eva; mmodzi wa alembi akale kwambiri, “ana sevente, ndipo iwo anali limodzi ana aamuna ndi aakazi.”

583 Tsopano, ngati . . . Ndiyeno ngati Kaini anapita ku dziko la Nodi . . . Tsopano, ngati inu mungazindikire, mlembi anali kwambiri, kulemba mwaluntha apa. Kodi inu munazindikira momwe iye anazibwereza izo?

Mu Edeni, pamene iwo anali ndi ana awo mu Edeni . . .

Tsopano, osati mMunda wa Edeni, wolembayu amadziwa izo. Yense yemwe analemba kolembedwaka apa, anati:

Pamene Adamu ndi Eva anali ndi ana awo mu Edeni . . .

584 Osati mMunda wa Edeni, chifukwa iwo anali atathamangitsidwa nachotsedwa ku Munda wa Edeni. Koma iwo anali apobe mu Edeni, ndipo Munda wa Edeni unali kummawa kwa Edeni. Koma Edeni anali ngati boma k—kapena

chiani. . . kapena dziko, ndiyeno Nodi linali dela lina kapena boma loyandikana kwa ilo.

585 Tsopano, munthu yekha yemwe Kaini akanakhala naye, kapena kumukwatira, akanayenera kukhala ali mchemwali wake yemwe. An kayenera kutero. Chifukwa panali mwamuna mmodzi yekha ndi mkazi komwe iwo akanakhoza kuchokerako, mwaona, ndipo iye ankayenera kuti amkwatire mlongo wake yemwe. Tsopano, izo zinali zovomerezeka mu masiku amenewo.

586 Ndipo Isaki anakwatira msuweni wake woyamba wakuchimuna, Rebeka, wodzozedwa ndi Mulungu. Sara anali mchemwali wa Abrahamu, mlongo wake mwa magazi; osati kwa amayi ake, kwa abambo ake. Mwaona, mlongo wake mwa magazi y—yemwe Abrahamu anamkwatira; amayi osiyana, koma bambo yemweyo.

587 Kotero, inu mukuona, kukwatirana mwa chibale apo, usanali—msempha wa magazi usanafooketsedwe mu mtundu wa anthu, chinali chololedwa ndi chabwino bwino. Tsopano izo siziri. Ngati iwe ukanati ukwatire mlongo wako lero, ndi kukhala naye ana, iwo mwinamwake akanakhala. . . chabwino, iwo akanangokhala opunduka ndi chirichonse. Ngakhale mpaka kwa msuweni wakuchimuna ndi wakuchikazi asamati azikwatirana, mwaona, chifukwa mtsinje wa magazi ukuyamba kukhala wotsika ndi kuyenda motsika.

588 Koma chinthu chokha apo chimene Kaini akanakhoza kuchichita, chikanakhala, kukwatira mchemwali wake yemwe. Ndipo apo npamene ana anali kuti. . . Iye anamutenga mkazi wake, anapita ku dziko la Nodi ndipo anakamudziwa iye, ndipo kuchokera apo kunabwera—ana. Mwaona, a. . .

589 Ndipo ngati inu mungazindikire, kuchokera mu mzere wa Kaini kunabwera anthu anzeru. Kuchokera mu mzere wa Seti kunabwera anthu achipembedzo, ine ndikutanthauza, m—mpesa wa chilungamo. Apo pomwe, awiri awo, anabweretsa apo mzere womwe amene ife tiri kukhalamo lero.

590 Ngati inu mungazindikire lero tsopano (pongotsirizitsa funso ili): kuti mzere wa Kaini uwo ukadalipo, ndi mzere wa Seti ulipo panobe. Onsewo anabwera mmusi chimodzimidzi basi. Ana a Kaini ali muno mu Jeffersonville usikuuno, ndipo ana a Seti ali muno mu Jeffersonville usikuuno. Pamene mtsinje wa magazi ukufooketsedwa ndi kumatha, koma mzere uwo ukukangamira apobe.

591 Tsopano, penyani. Ana a Kaini anali nthawizonse. . . ndipo chisanachitike chionongeko cha chigumula, iwo anali anthu anzeru: asayansi, ophunzitsa; ndi achipembedzo kwambiri, koma anali gulu lotsutsidwa. Mwaona? Tsopano penyani, iwo anali basi monga bambo wao Kaini. Kaini, iye anali munthu wachipembedzo. Iye anamanga guwa lokongola, ndipo anapanga mpingo wokongola, ndipo anayesera kuzipanga izo

kukhala zowoneka mokongolerapo kuposa mishoni yaing'ono iyo yomwe Seti anali nayo kumeneko. Kodi inu mumadziwa izo? Iye ndithudi. . . Iye analikongoletsa guwa ndi maluwa, ndi kulikonza ilo mokongola, ndipo analipanga ilo kukongola; ndipo anapanga mpingo wawukulu, wamphamvu, wofufuma, chifukwa iye ankaganiza kuti akanapeza kukondedwa ndi Mulungu pakuchita choncho.

⁵⁹² Ndipo Abele anapita uko ndipo anakatenga mwanawankhosa wamng'ono, ndipo anayamba kumukokera iye ku guwa uko, ndipo anamugoneka iye pa thanthwe namupha iye.

⁵⁹³ Ndipo tsopano, ngati Mulungu pokhala wolungama, ngati zonse zomwe Iye ankafuna zinali kupembedza, Kaini anapembedza Mulungu ndi kuwonamtima kochuluka basi monga Abele anachitira. Onse awo anali owonamtima. Onse awo anali kuyesera kuti apeze chisomo ndi Mulungu. Iwo panalibe mmodzi wa iwo wachikunja. Iwo onse anali, mwamtheradi, okhulupirira mwa Yehova. Tsopano, apo, izo zikutipatsa ife chinachake choti tichiganizire.

⁵⁹⁴ Ena pano usikuuno ine sindinayambe ndawaonapo, anthu; ine sindinayambe ndakuonanipo inu kale. Koma inu muyenera kuzindikira ichi, ndi kuchisunga ichi mu malingaliro anu. Mwaona? Ziribe kanthu momwe inu muliri achipembedzo, izo ziribe kanthu kamodzi kochita nazo. Inu mukhoza kumakhala mu mpingo, inu mukhoza kumakhala nthawizonse owonamtima, ndipo inu nkukhalabe wotaika! Mwaona?

⁵⁹⁵ Ndipo inu mukuti, “Chabwino,” inu mukuti, “abusa athu ndi ophunzira kwambiri, iwo anabwera kupyolera ku maseminare kuti apeze maphunziro opambana. Iwo ndi afioloje, iwo amaidziwa f—fioloje yonse ndi zina zotero. Ndipo iwo ndi anzeru, ophunzitsidwa, o . . . osankhidwa opambana omwe ife tikuwadziwa.” Ndipo iwo akhoza kukhala ali otaikabe! Mukuona?

⁵⁹⁶ Tsopano Kaini, pa mzere wake: iwo anali, aliyense, achipembedzo kwambiri; anthu otchuka kwambiri; ndipo iwo anali asayansi, ndi madotolo, ndi omanga, ndi ogwira ntchito, ndi anthu anzeru. Koma m'badwo wonse uwo unakanidwa, kuchokera kwa Kaini njira yonse mpaka pansu.

⁵⁹⁷ Ndipo ku mbali ya Abele: iwo sanali omanga ngakhale ophunzitsa kapena anthu ophunzira; iwo anali, mochuluka kapena mochepera, onyozeka, mtundu woweta nkhusa, ndi amphawi, omwe ankangoyenda mwa Mzimu.

⁵⁹⁸ Tsopano, Baibulo linati, “Palibe kutsutsika kwa iwo omwe ali mwa Khristu Yesu, omwe samayenda mwa thupi koma mwa Mzimu.” Munthu wauzimu ali ndi solo yauzimu yomwe siingakhoze kufa. Ndipo munthu wachithupithupi ali ndi chikhaliwe cha chipembedzo pa iye (ndipo amafuna kupembedza ndi zina zotero) koma iye ndi wachithupithupi;

osati wosakhulupirira, koma wokhulupirira mwachithupithupi; ndipo uwo unali mtundu womwe unakanidwa.

599 Tsopano, kuchokera uko, Kaini anapita ndipo anakamkwatira mkazi wake mu dziko la Nodi. Tsopano, ilo silimanena yemwe Seti anamukwatira, kapena yemwe enawo anawakwatira. Ndipo chinthu chokongola kwambiri cha izo ndi kudziwa kuti—kuti, kukwatira kwa Kaini, ife tiri nako yankho lake. Chifukwa iye ankayenera kuti akwatire mlongo wake, kapena iye . . . kapena apo pakanakhala pali . . .

600 Panalibe akazi ena pa dziko lapansi, koma basi ankayenera kuti abwere kuchokera kwa Eva. Iye anali mayi wa amoyo onse. Ndiwo anthu onse omwe anali amoyo, iye anali mayi wa iwo. Ndi chifukwa chake iye anali . . . Mawu oti *Eva* amatanthauza “mayi wa amoyo.” Kotero iye anabwera ndipo anabala mwana uyu. Ndipo Kaini anamkwatira mlongo wake yemwe, ikanakhala njira yokha yomwe ine ndikanawonera pa izo. Chotero analipo anthu omwe anali moyo mu tsiku limenelo, zoonā. Mwaona? Chabwino, ndi . . .

Pamene Adamu ndi Eva anali ndi ana awo mu Edeni . . .
Tsopano penyani, ndilo funsolo: **Pamene iwo anali ndi ana awo mu Edeni, kodi panali anthu ena pa dziko lapansi pa nthawi iyi? Ayi! Ndiye mu Genesis 5:16, inu mukuona, Kaini anakakhala mu dziko la Nodi ndipo anakamudziwa mkazi wake.** Zedi. Mwaona?

601 Ameneyo ndi Genesis 1, pamene Iye anamulenga munthu mwa chifanizo Chake Chomwe, chomwe chinali mwa fiofane. Ndipo mu Genesis 2, Iye anamupanga munthu kuchokera mu fumbi la mdziko lapansi, yemwe anali munthu wathupi yemwe ife tiri naye tsopano. Ndiyeno, mu 3 munali kugwa, ndipo anathamangitsidwa kuchokera mMunda wa Edeni; ndiyeno anawo anabala ana. Ndipo Kaini anamutenga mkazi wake nakakhala naye mu dziko la Nodi, kunjā, chifukwa Mulungu anali atamulekanitsa iye ku chiyanjano ndi m’bale wake yemwe (chifukwa cha imfa y—ya Abele). Ndipo ndi yemwe iye anali naye, mlongo wake yemwe, ndipo anamukwatira iye; ndi njira yokha yomwe ine ndingakhoze, pandekha, ndingakhoze kuwona momwe k—momwe iye anakwatirira.

602 Tsopano, izo zakhala zikunenedwa . . . Ndipo ine ndikuyembekeza kuti amzanga achikuda omwe ali muno akhululukira ndemanga iyi, chifukwa mwamtheradi si zolondola. Nthawi yoyamba yomwe ine ndinayamba ndakomana naye konse mmodzi wina mu moyo wanga, ine nditatembenuka kale . . . ine ndinali . . . ndinakomana ndi M’bale George DeArk ndi iwo kumusi uko. Ndipo ine ndinali kuyenda, ndipo Ambuye ananditsogolera ine ku malo aang’ono. Ndipo iwo anali akukambirana komwe munthu wakuda anachokera. Ndipo iwo anali kuyesera kunena kuti munthu wakuda . . . Kuti Kaini

anakwatira chinyama chonga nyani, ndipo kuchokera apo kunabwera mtundu wa anthu akuda. Tsopano, uko nkulakwitsa! Mwamtheradi, uko nkulakwitsa! Ndipo musati konse muziimira izo. Chifukwa kunalibe wachikuda kapena mzungu, kapena wina aliyense wosiyana, ndi mtundu umodzi wokha wa anthu mpaka ku chigumula. Ndiye chitachitika chigumula ndi nsanja ya Babulo, pamene iwo anayamba kumwazikana, ndi pamene iwo anatenga mitundu yawo ndi zina zotero. Iwo onse anachokera ku mtengo wofanana. Ndizo ndendende kulondola. Adamu ndi Eva anali bambo wawo ndi mawo, mwapadziko, wa chamoyo cholengedwa chirichonse cha anthu okhalapo omwe anayamba akhala moyo pa dziko lapansi. Ndiko kulondola. Okuda, oyera, otuwa, abulauni, achikasu, mtundu uliwonse womwe inu mungakhale muli, izo ndi mwamtheradi malo omwe inu mukukhalako, ndi momwe k—kuti . . . Monga ngati . . .

⁶⁰³ Ine ndikuganiza ine ndikhoza kufotokoza izi pamene ine ndiri pa izo. Anthu pano tsopano mu kusankhana uku ndi malamulo ndi zinthu zomwe iwo akuzikhazikitsa, ine ndikuganiza ndi zopusa. Ine ndikutero kwenikweni. Mvetserani, ingowasiyani anthu amenewo okha, iwo akudziwa chomwe iwo akufuna. Mulungu anamupanga munthu wakuda, ndipo iye ndi wokondwa nazo. Mwamtheradi! Ngati Mulungu akanandipanga ine kukhala munthu wakuda, ine ndikanakhala wosangalala nazo; ngati Iye akanandipanga ine munthu wabulauni, ine ndikanakhala ndiri wokondwa; ngati Iye akanandipanga ine munthu woyera, ine ndikanakhala ndiri wokondwa; ngati Iye akanandipanga ine munthu wachikasu, ine ndikanakhala ndiri wokondwa. Mulungu anatipanga ife mu mitundu yathu, ndipo Iye anatipanga ife momwe Iye ankatifunira ife, ndipo ndife tonse ana Ake. Mwamtheradi! Ndipo iwo samayenera kuti azikangana ndi kumapitiriza nazo monga choncho. Ndi kulakwitsa kumachita zimenezo. Iwo sayenera kuti azichita izo. Mulungu anatipanga ife . . . momwe ife tikufunira izo.

⁶⁰⁴ Ndipo munthu wachikuda, iye samafuna kuti azipita kunja uko ndi kumauswa m—m’badwo wake kapena mtundu wake, ndi kukusakaniza iwo ndi woyera ndi chirichonse monga choncho. Ine sindikumutsutsa iye. Ine sindiri. Munthu wakuda ali nazo zinthu zomwe munthu woyera alibe nkomwe. Mwamtheradi! Ndi kulondola ndendende. Ndipo Mulungu sanalinge kuti iwo azikhala mwanjira imeneyo.

⁶⁰⁵ Chabwino, taonani. Munthu wachikuda ali . . . i—iye ali . . . iye ali ndi—iye ali ndi kaonekedwe pa iye komwe munthu woyera samakhala nako konse. Iye ali nako kukondwa komupatsa mwayi, “kudalira Mulungu, ndi kungolola zonse zina kuti zizipita”; kaya ali nazo kapena alibe, iye amakhala wokondwa mulimonse. Ine ndikanafuna ndikanakhala ndi zochuluka za izo, usikuuno, ine ndikutsimikiza ndikanatero. Chabwino, iye ali nazo izo, ndipo icho ndi chake chake; iwo samafuna kuti

azidzisanika ndi mtundu wina wa anthu ndi kuziswa izo, ngakhalenso. Ndi ndendende kulondola.

⁶⁰⁶ Ine ndikuganiza dona kumusi uko ku Shreveport anapanga imodzi yopambana—ndemanga yopambana yomwe ine ndinayamba ndaimvapo mu moyo wanga. Iye anapanga ndemanga, ndipo iwo anaiika iyo mu pepala. Iye anapita apo, iye anati, “Momwe zinthu izi zikuchitikira muno, mu kusankhana uku, ine sindikufuna kuti ana anga azipita ku sukulu ku sukulu ya oyera awo.” Anati, “Iwo sakakhala ndi kusamalidwa komwe iwo akanakhala nako ngati iwo akadakhala ndi mphunzitsi wachikuda.” Mkazi uyo ndi mkazi wanzeru. Iye amadziwa chomwe iye amachiyankhula, iwo amapeza maphunziro abwinoko. Ndi kulondola ndendende. Chotero ine ndikuganiza anthu akuchita molakwitsa pakuchita zimenezo.

⁶⁰⁷ Ndiyeno iwo amati, “Kaini ndi Abele. . .” ndi zina zotero monga choncho. Ayi, bwana! Khungu linalibe kanthu kochita nazo. Ndi mzimu mkati mwakemo umene uli ndi chinachake chochita nazo. Ndi kulondola ndendende.

⁶⁰⁸ Kotero Kaini anamudziwa mkazi wake, ndipo uyo anali mlongo wake. Ndipo iwo. . . iye anamutengera iye ku dziko la Nodi, ndipo uko kunabadwa mitundu yopambana ya pa dziko: azachipembedza ndi opembedza.

⁶⁰⁹ Ndipo tangoganiza lero, mzanga, tangoima ndi kuganiza kwa kamphindi kokha. Kuti alipo makumi a zikwi kuchulukitsa makumi a zikwi ndi zikwi za zikwi, za mwamtheradi anthu opita ku mpingo, owoona mtima basi ndi odzipereka kwa mpingo umenewo momwe iwo akanakhala ali, omwe ali otaika basi momwe Kaini analiri. Mwaona? Ndi Mulungu yemwe amasankha! Ndi Mulungu yemwe amapatula! Mwaona? Mulungu yemwe amapereka chifundo! Dongo silingakhoze kunena kwa woumba, ndi woumba pa dongo. Ndiko kulondola.

⁶¹⁰ Tsopano apo pali lina lokongola, lotsatira lake apa:

Mu II Petro 2:4—2:4 . . .

⁶¹¹ Winawake ali ndi Baibulo, akufuna kuti atembukire ku malemba awa mofulumira kwambiri pamene ine ndikuwawerenga iwo, ngati inu mukufuna kutero. Ndipo mukhala ngati mukundithandizira ine limodzi pano, pamene ife tikulitenga funso ili.

⁶¹² Tsopano, pa Kaini uyu n—ndi zina zotero, ngati izo sizikukhutitsa icho tsopano, inu mungotilola ife tikhale nazo. Ife tikhala okondwa. . .

⁶¹³ Tsopano II Petro 2:4. Chabwino, bwana, ndi ife apa:

66. II Petro 2:4. “Pakuti ngati Mulungu ali. . . Pakuti ngati Mulungu sanawalekerere angelo omwe anachimwa, koma anawaponyera iwo pansu mu gehena,” ndiye nchifukwa

chiani Yesu anakalalikira kwa mizimu mu ndende, mu I Petro 3:19?

614 Tsopano, ife tapeza Petro 2:4, poyamba. Chabwino:

Pakuti ngati Mulungu sanawalekerere angelo omwe anachimwawo, koma anawaponyera iwo p—pansi ku hade, n—ndipo anawapereka iwo ku unyolo wa mdima, kuti asungidwe kufikira chiweruzo;

615 Tsopano, tsopano tiyeni tipeze mu I Petro, (uyo ndi II Petro). I Petro 3:19, mvetserani kwa izi. Ndi ife apa, pomwepa. Izi zangobwera, nchifukwa chake ine sindinazilembe izo.

...yemwe aponso...anapita nakalalikira kwa mizimu mu ndende;

616 O, inde, ndi ife apa. Tiyeni tiyambire pang’ono tisanafike apo, ndime ya 18:

Pakuti Khristu nayenso...anazunzikapo chifukwa cha machimo, wolungama chifukwa cha osalungama, kuti iye akhoze kutibweretsa ife kwa Mulungu, poikidwa ku imfa mu thupi, koma anafulumizitsidwa ndi Mzimu:

Momwe Iye anapitanso nakalalikira kwa mizimu ya mu ndende;

Yomwe nthawiina inali yosamvera, . . .

617 Mzanga wokonedwa, ngati iwe utangowerenga ndime yotsatirayo, ndipo apo Iwo akuzifotokoza izo. Mwaona?

Omwe nthawiyina anali osamvera, omwe nthawiyina kupirira motalika kwa Mulungu kunadikira mu masiku a Nowa, pamene chombo chinali nkukonzedwa, momwe ochepa, omwe ali, miyoyo isanu ndi itatu anapulumutsidwa ndi madzi. (mwaona?)

618 Tsopano, ngati inu mungazindikire mkati umu, ine ndikuganiza mlaliki uyu ali nalo lina pa...chinachake mu mzere womwewo, chiti chiyankhidwe patsogolo pang’ono.

619 I Petro 4...kapena 2:4, ngati inu mungazindikire, “pakuti ngati Mulungu sanawalekerere angelo,” kodi *mngelo* uyo walembedwa bwanji? “m” wamng’ono. Mwaona? Tsopano, cha apa, “mizimu yomwe inali mu ndende yomwe siinalape mu kupirira kotalika kwa masiku a Nowa,” *mngelo* yemweyo. Awo anali anthu: atumiki, alaliki; “sanawalekerere angelo.” Kodi inu mumadziwa kuti...mawu oti *mngelo* amachokera ku mawu oti “mthenga”? Ndi angati amadziwa kuti *mngelo* ndi “mthenga”? Mwamtheradi, *mngelo* ndi mthenga, “ndipo Iye sanawalekerere angelo.” Mwaona?

620 Ndipo cha apa mu Ahebri, inu mukukumbukira kuti ife tinadutsa mu izo masabata pang’ono apitawo, “angelo”?

621 Ndipo umu Iye-. . .mu Chivumbulutso, “Kwa mngelo wa mpingo wa Sarde lemba zinthu izi. Kwa mngelo wa mpingo wa Aefeso lemba zinthu izi. Kwa mngelo wa mpingo. . .” Mukukumbukira izo? Ndipo ife tinayendetsa mawu oti *mngelo* chammbuyo, ndipo kuchokera mu dikishonare, ndipo tinapeza kuti izo zimatanthauza “mtumiki.” Iye akanakhoza kukhala “mtumiki pa dziko lapansi, mtumiki wauzimu,” mawu oti *mngelo*.

622 Chotero mu chikhalidwe ichi, ngati ife titatenga lexicon ndi kufufuza umu, inu mungapeze kuti zikuyambira kwa “atumiki, atumiki oyamba.” Mwaona, “Ngati a. . .Ngati iye sanawalekerere. . .Pakuti ngati Mulungu sanawalekerere angelo omwe anachimwa,” (mwaona?) “ndipo zinthu zauzimu,” (mwaona?) “atadikirira kaye. . .”

Tsopano penyani, iye anati:

. . .*ngati. . .sanawalekerere angelo omwe anachimwawo, koma anawaponyera iwo ku hade, ndipo anawapereka iwo ku unyolo wa mu mdima, kuti akasungidwe kufikira chiweruzo;*

623 Ndiye yang’anani uko mu I Petro apa kachiwiri, 3:19, penyani momwe izi zikuwerengekera tsopano:

Pakuti *potero iye anapita nakalalikira kwa mizimu mu ndende;*

Yomwe nthawiyina inali yosamvera, pamene pena mwa kupirira motalika kwa Mulungu kunkayembekezera mu masiku a Nowa. . .(mwaona, iwo anali atumiki a tsiku limenelo, atumiki). . . pamene chombo chinali kukonzedwa, mmene. . .izo nkuti, miyoyo isanu ndi itatu inapulumutsidwa ndi madzi.

624 Tsopano ngati inu mungazindikire pamene zolengedwa izo zinali Kumwamba. Tsopano, uko mu Chivumbulutso 11. . . kapena mutu wa 7, ine ndikukhulupirira. . .kapena ayi, ayi, ndi mutu wa 12. Iye akupereka chithunzi cha mkazi ataima; mwezi uli pa mutu wake ndi dzuwa. . .kapena, dzuwa liri pa mutu wake ndi mwezi pansu pa mapazi ake. Ndipo chinjoka chofiira chinaima kuti chimulikhwire mwanayo mwamsanga pamene iye akanabadwa, ndipo iye anatenga mchira wake nakoka gawo limodzi pa atatu a nyenyezi za Kumwamba ndipo anaziponyera izo ku dziko lapansi. Kodi inu munazindikira izo? Tsopano, izo sizikutanthauza kuti Satana ali ndi—mchira wautali womwe amakola mowazunguliza nawo anthu, koma “nthano yomwe iye *anazinena*,” ndipo anakokera gawo limodzi mwa achitatu a nyenyezi zimenezo. Nyenyezi zimenezo zinali mbewu ya Abrahamu.

625 Abrahamu anati, “O. . .”

626 Mulungu anamuza Abrahamu, “Yang’ana mmwamba ku miyamba, ndi kuziwerenga nyenyezi ngati iwe ungate.”

627 Iye anati, “Ine sindingathe kuchita izo.”

628 Iye anati, “Sudzakhoza ngakhalenso kukwanitsa kuziwerengera mbewu zako,” nyenyezi.

629 N’ndani ali Nyenyezi yowala ya Mmawa? Yesu waku Nazareti, yowalitsitsa yomwe inayamba yakhalapo mu mnofu wa umunthu. Iye ndi Nyenyezi yowala ya Mmawa. Ndipo Iye ndi Mbewu ya Abrahamu, yobwera kupyolera mwa Isaki. Ndipo ife, pokhala okufa mwa Khristu, timatenga Mbewu ya Abrahamu ndipo ndife olandira molingana ndi lonjezo.

630 Koteronyenyezi za kumwamba zinkaimira mizimu ya anthu kuno. Ndipo pamene chinjoka chofiira (Roma, pansipakuzunza kwake) chinakumbatira mwa icho magawo awiri a atatu a . . . kapena gawo limodzi pa atatu a nyenyezi, ndipo anaziponyera izo pansipakuzunza, izo zinali pa kupachikidwa kwa Ambuye wathu Yesu pamene iwo anamukana Iye ndipo Iye anali . . . ndipo anamuponyera Iye kunjandipo analibe kanthukochita ndi Iye; apo panali gawo lachitatu ilo la nyenyezi zaungelo, zokhalapo zaungelo.

631 Taonani, mu thupi lanu, mkati mwa inu . . . (ife tiri ndi funso lina pa izo, molunjika, kuti tiziyankhe izo mwabwinoko). Chotero pamene . . . Mkati mwa inu muli mzimu, munthu wina. Kunjaka kwa inu kuli munthu mmodzi, mkati mwa inu muli munthu wina. Koteromkati mwa inu ndi wauzimu, kunjaka kwa inu ndi wogwirika. Mukuona? Ndipo chinthu ichi, ngati inu muli wotsogozedwa ndi Mzimu, mwa Mulungu, inu munakhala mtumiki wa Mulungu, kapenamngelo. *Mtumiki* wa Mulungu, *mngelo* wa Mulungu, ndi mawu omweomwewo; simungakhoze kuwalekanitsa iwo: Mtumiki wa Mulungu, kapena, mngelo wa Mulungu.

632 Ndipo ndi uti yemwe ali ndi ulamuliro waukulu kwambiri? Mngelo wochokera Kumwamba kapenamngelo wa pa guwa? Ndi uti ali nawo iwo? Mngelo wapa guwa! Paulo anati, “Ngati mngelo wochokera Kumwamba abwera nadzalalikira uthenga wina uliwonse kwa inu wosiyana ndi uwo umene ine ndaulalikira kale, msiyeni iye akhale wotembereredwa.” Chotero mngelo wodzozedwa ndi Mzimu Woyera ndi Mawu amaima pafupi ndi Mulungu. Ndiko kulondola. Kumwamba, ulamuliro wake . . .

633 “Mphamvu zonse Kumwamba ndi pa dziko lapansi zapatsidwa mu dzanja Langa. Pitani, ndipo ine ndizipita nanu. Chirichonse chomwe inu muti muzimanga pa dziko lapansi, ine ndizichimanga Kumwamba. Chimene inu muchimasula pa dziko lapansi, Ine ndizichimasula Kumwamba.”

634 O, ngati Mpingo waukulu woyera ukanangozindikira mphamvu yake kuti uzichitira zinthu izi. Koma pali kukaikira kochulukana ndi mantha ndi kunjenjemera, kudabwa ngati izo

zingatero, “Kodi zingakhoze kuchitika?” Utali wonse pamene izo zizikhalapo, Mpingo sungakhoze kuimirira chiriri. Ndipo pamene kuyankhula konse kwa mantha kuchoka ndipo Mzimu Woyera ukakhala mu ulamuliro wathunthu kwa Mpingo, ndiye mantha onse amachoka, ndipo Mpingo umenewo uli nayo mphamvu. Mwaona? Bwanji, iwo ali nacho chirichonse chomwe Kumwamba kuli nacho kumbuyo kwawo. Iwo ndi akazembe a Mpandowachifumu. Mwamtheradi! Kazembe wa Khristu ali nawo ulamuliro, ndipo zonse zomwe Khristu ali nazo ndi za kazembe ameneyo. Ndipo Iye anati, “Pitani inu ku dziko lonse, inu mukhala mboni Zanga Mzimu Woyera ukabwera pa inu.” Ndipo kodi mboni ndi chiani? Ndi kazembe; ndiko kubwera kudzachitira umboni chinachake. Mphamvu zonse za Kumwamba ziri mmanja mwanu momwe! O, kodi ife timakhalira chiani? Ndipo mpingo uli wouma, ndipo ife tikukhala matalala. Ndi chifukwa kuti ife sitimazizindikira zinthu izi.

⁶³⁵ Tsopano, miyoyo yomwe inali mu ndende (yomwe siinalape), siinali zinthu Zaungelo zomwe zinali—omwe anatsitsidwa pansi mwa mawonekedwe Angelo, koma iyo inali mizimu ya zinthu zaungelo izo zomwe zinagwa asanaikidwe maziko a dziko, mmbuyo umo pamene nkondo inachitika Kumwambako. Ndipo Satana n—ndi chinjoka anamenyana, ndiyeno . . . kapena Mikaeli n—ndi—chinjoka anamenyana (ndi Lusifara). Ndipo Lusifara anaponyedwa kunja ndi ana ake onse (angelo onse omwe iye anali atawanyenga), ndipo angelo amenewo anabwera ku dziko lapansi ndipo anali woti akhale anthu apono. Ndipo pamene iwo anatero, ndi pamene “ana a Mulungu anawona ana aakazi a anthu kuti anali okongola, ndipo anadzitengera kwa iwo akazi.”

⁶³⁶ Iwo ndi ana aamuna a Mulungu. Mwamuna aliyense yemwe amabadwa mu dziko lapansi lino ndi mwana wa Mulungu. Mosasamala kaya iye ndi wochimwa kapena chomwe iye ali, iye ndi mwana wa Mulungu. Analengedwa mwa maonekedwe a Mulungu kwa matamando a Mulungu, iye analengedwa mwanjira imeneyo. Koma Mulungu pachiyambi ankadziwa yemwe akanati adzamulandire Iye ndi yemwe akanati asadzamulandire Iye. Kotero Iye akanadzakhoza kukonzeratu . . . kapena osati kukonzeratu, koma mwakudziwiratu Iye akanakhoza kudziwa yemwe akanati adzapulumutsidwe ndi yemwe sakanati adzapulumutsidwe, pakuti Iye ankadziwa munthu yemwe akanati adzatenge mzimu uti.

⁶³⁷ Ndipo mizimu iyo yomwe inatuluka kuchokera ku Mpandowachifumu wa Mulungu, ndipo inkaima pamaso pa Mpandowachifumu wa Mulungu, ndipo imakhalapo . . . ndi mabilioni ndi mabilioni ndi nthawi zosawerengeka dziko lisanayambe nkomwe, mu Kukhalapo kwa Mulungu, kodi inu muganiza kuti iwo samadziwa chinachake cha kupembedza?

Ndipo iwo anabwera pansi nadzalowa mwa anthu momwe, ndipo iwo amamupembedza Mulungu! Mwamtheradi, iwo amamupembedza Mulungu; ndipo iwo ali nacho chidziwitso cha Mulungu, ndipo iwo ndi anzeru, ndi othyathyalika, ndi ophunzira, nthawizonse. Koma Mulungu anawakana iwo kuchokera kuchiyambi!

⁶³⁸ Koteru choncho, mzanga, umembala wa mpingo, k—kapena chidziwitso cha fioloje ina kapena chinachake, ziribe chinthu chimodzi chochita ndi Izo. Ayenera kukhala ali Magazi a Yesu Khristu ndi kubadwa kwatsopano komwe kumakulumikizani inu kwa Iye ngati munthu mmodzi. Ndi inu apo.

⁶³⁹ Mulungu, pachiyambi pamene Iye anadziwa izo... Mwamuna ndi mkazi uyo anapangidwa mmodzi, osati awiri, iwo anapangidwa mmodzi. Iwo analekanitsidwa, mmodzi anaikidwa mu mnofu ndi winayo mu fiofane. Iye ankazidziwa izo. Chotero polinga kuti atsimikizire izo kwa inu: pamene Mulungu anamupanga mkazi, Iye sanachite kutenga fumbi lina ndi kumupanga iye momwe Iye anachitira ndi mwamuna; Iye anatenga nthiti kuchokera ku mbali ya Adamu, ndipo iye anakhala chochokera kwa mwamuna (chifukwa iye ndi gawo la iye). Inu mukuzimvetisa Izo tsopano? Mwaona? Ndi inu apo.

⁶⁴⁰ Ndi awo angelo apo. Ndipo Mulungu ndi mzimu womwe umalumikizana ndi Mulungu ndi Mzimu umodzi. Ndiko kulondola. Tsopano, Mzimu wa Mulungu umene ukukhala mu Mpingo, ndi Mzimu umene umachokera Kumwamba, umene Mulungu anawudziwa asanaikidwe maziko a dziko, umene unalikhana bodza la Mdierekezi. Ndipo mzimu umenewo unachita kutenga thupi la mnofu kuti ukhale...kuti atenge kuyesedwa kwake. Iwo unachita kudzakhalala thupi monga ina iyi inachitira, ndipo yonseyo yaikidwa pa goli limodzi. Ndipo Mulungu, pachiyambi pomwe, ankaidziwa mizimu yomwe ikanati, ndi yomwe siikanadzati. Ndi inu apo. Mdierekezi ndi wanzeru kwambiri iye basi...nyenge osankhidwa omwe, ngati zikanatheka.

⁶⁴¹ Koteru mizimu iyi, angelo awa omwe analalikhira, inali mu ndende; *angelo*, ngati inu mungazindikire izo apa, ndi “a” wamng’ono chomwe chikutanthauza “anthu”; angelo, atumiki kuno padziko lapansi. Iwo anachimwa, ndipo njira yokha yomwe iwo akanati achimwire ikanakhala ili kusakhulupirira! Ndipo njira...Iwo anali nazo zipembedzo zawo zawo, ndipo iwo sanawukhulupirire uthenga wa Nowa. Iwo sanawukhulupirire uthenga wa Enoki. Ndipo iwo anawukana Uthenga wawo, “ndipo anaweruzidwa,” Baibulo limati iwo anatero.

⁶⁴² Enoki ananenera kwa iwo, anati, “Ambuye akudza ndi zikwi makumi a oyera Ake.”

⁶⁴³ Ndipo iwo ananenera. Ndipo Nowa anamanga chombo, ndipo iwo ankati, “Iye ndi woyera wodzigudubuza! Iye ndi

wotentheka! Palibe chinthu chotero ngati mvula kubwera.” Ndipo zaka handiredi n twente zinapitapo, ndipo iye anali ndi chipembedzo chomwe chinali ndi chipulumutso mwa icho, panali njira yothawirapo itapangidwa, koma iwo anali okhutitsidwa mu chikhalidwe chawo.

644 Ndi momwe izo ziliri lero, kuti anthu akukhutitsidwa ndi chikhalidwe chawo. Koma pali njira yothawira, ndipo njira imeneyo ndi kudzera mwa Yesu Khristu. Amen. Ndi inu apo: mtundu womwewo, mizimu yomweyo.

645 Ndipo iwo anali mwamtheradi anthu achipembedzo, achipembedzo kwambiri, koma iwo anaphonya lumbiro la pangano.

646 Chomwechonso izo ziri lero. Anthu amapita ku mpingo, ndi kujowina mipingo yaikulu, ndi kumayesera kuti akhale munthu wotchuka kwambiri mu mzindawo. Ngati iwo akufuna kuti ajowine mpingo, iwo amakapeza waukulu kwambiri mu mzindawo, wopambana ndi woganiziridwa-bwino mu mzindawo. Kutalikirana kwake momwe iwo amakuphonyera kuitana! Kutalikira kwake momwe iwo amaziphonyera Izo!

647 Njira yokha yomwe inu muti mudzamudziwire konse Yesu Khristu ndi mwa vumbulutso lauzimu, osati mwa fioloje ndi kuchuluka kwa momwe inu mumawerengera Baibulo. Kaya ndinu wa Christian Science, Methodist, Mboni za Yehova, kapena chirichonse chomwe inu muli; ziribe kanthu chomwe inu muli, inu simudzadziwa konse Izo mwa Mawu, ndi Mzimu wa Mulungu umene umamuwululira Iye kwa inu. Ndi vumbulutso lauzimu!

648 Pamene Adamu (mMunda wa Edeni) ndi Eva... pamene ana awo anaponyedwa kunja, apa panadza Kaini ndi fioloje yabwino. Iye anati, “Mulungu ayenera kudziwa kuti ife tikuchita izi kuchokera ku—kupambana kwa mtima wanga. Ine ndimanga guwa lokongola, ine ndiika maluwa pa ilo, ine ndiika zipatso pa ilo, ine ndilipanga ilo mokongola. Ndithudi ine ndikhoza kumukondweretsa Mulungu ndi izi ndi kumulola Iye kuti adziwe kuti ndine wodzipereka mu mtima wanga.” Iye anali kulondola monga momwe Mawu ankapitira; Mulungu ankafuna kupembedzedwa, iye anapita kumakapembedza. Iye anapanga malo okongola kuti azipembedzerapo, aakulu, chinyumba chabwino (monga iwo amazitchera izo lero). Ndipo iye anazipanga izo molondola, iye anazimanga izo molondola naika guwa mmenemo; iye sanali wachikunja.

649 Koma Abele, pa Mawu a Mulungu... Panalibe Baibulo litalembedwa apo, koma Mulungu ANAWULULA kwa iye kuti sichinali chipatso chimene chinatitulutsa ife mmunda wa Edeni, siinali apulo imene Adamu ndi Eva anadya, zinali mwamtheradi zinthu zakugonana zomwe zinawalekanitsa iwo ndi kuwagawaniza iwo. Ndipo podziwa kuti anakhala achivundi,

ndi podzera mmagazi a Adamu, ndipo kupyolera mmagazi a serpenti omwe anayambitsa izi, Abele, mwa vumbulutso Laumulungu, anapita ndipo anakatenga mwanawankhosa namupereka iye. Ndipo Mulungu anati, “Ndi Zimenezo!” Ndithudi.

650 Pamene iwo ankatsika pa Phiri Lachiwalitsiro, Yesu anati, “Kodi anthu amati Ine Mwana wa munthu ndine yani?”

651 “Ena amati Ndinu ‘Mose,’ ndipo ena amati Ndinu ‘Eliya,’ ndipo ena amati Ndinu ‘Yeremia,’ ndipo ena amati Ndinu ‘mneneri uja.’”

652 Iye anati, “Koma inu mukuti ndine yani?”

653 Petro anati, “Ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu Wamoyo.”

654 Iye anati, “Wodala ndi iwe, Simoni Bar-yona, pakuti thupi ndi mwazi sizinaulule izi kwa iwe.” (Penyani!) “Osatinso kupyolera mu kalata, osatinso kupyolera mu sukulu; iwe sunaziphunzire izi ku seminare, ngakhalenso kuti wina anakuuza iwe. Thupi ndi mwazi sizinaululire izi kwa iwe, koma Atate Anga omwe ali Kumwamba aziwululira izi kwa iwe. Ndipo pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizingaulake pousutsa Iwo.” Ndi inu apo. Ndi uwo Mpingo wa Mulungu wamoyo. Ndi umenewo. Pa mpingo umenewo. . . Pa *vumbulutso* ilo, Mpingo uwu wamangidwapo. Ndi vumbulutso Lauzimu lomwe Mulungu waulula, kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu, ndipo inu mwamuvomereza Iye ngati Mpulumutsi wanu wanu, inu mwadutsa kuchokera ku imfa nkupita ku Moyo.

655 Ndipo Mzimu Woyera ukusuntha ndi kugwira ntchito mu ziwalo za Thupi ili. Ndi umenewo Mpingowo! Ziribe kanthu kaya iwo ndi wosauka, ndipo uli mu mishoni, ndipo inu mumaima kunjira pansu pa mtengo wa paini penapake, kapena kulikonse komwe iwo uli, ngati iwo uli mu nyumba ya winawake mu msonkhano wapadera, ziribe kanthu komwe iwo ungakhale uli. Kukongola ndi zinthu sizimamupepetula Mulungu. Ndi kuwonamtima kwa mtima mwa vumbulutso kuti Yesu Khristu waperekedwa ngati Mwana wa Mulungu, Mpulumutsi wathu wathu. Amen!

656 Mai, ife. . . iwe sungazitenge izi, nkutsiriza monga choncho, tingatero ife?

657 Ndi awo omwe. . . kumeneko komwe Iye anapita; angelo: atumiki, alaliki awo, aluntha awo, atumiki awo omwe sankakhulupirira pamene Nowa anapita kukalalikirira kwa iwo nawauza iwo, “Bwanji, bwerani mu chombo ichi.”

658 Iwo ankati, “Tamvetserani kwa woyera wodzigudubuza uyo. Tamvetserani kwa wotentheka uyo. Bwanji, kuno kulibe mvula. Ndani anayamba wamvapo chinthu choterocho? Bwanji, mai,

kodi ife tiribe mipingo? Kodi ife si achipembedzo?” Bwanji, iwo anali achipembedzo!

659 Yesu ananena kuti pakanakhala m’badwo umene anatha, mbadwo umenewo udzabwereza kachiwiri basi kusanachitike kudza Kwake, “Monga izo zinaliri mu masiku a Nowa, chomwecho zidzakhala ziri mu kudza kwa Mwana wa munthu. Pakuti iwo anali kudya, kumwa, kukwatira, kuperekedwa mu chikwati.” Iwo anali naye Reno, Nevada apo, kwinakwake. Iwo anali nayo mitundu yonse ya zachabechabe zomwe iwo ali nazo lero; kupikisana, kudzionetsera, ndi kupanga zosangalatsa, onyoza ndi ena otero; omakhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma akumakana Choonadi chenicheni: pangano, Uthenga wa chisomo. Mulungu akupanga njira Yake, ndi kuwapatsa anthu P—pangano Lake, momwe iwo akanati athawire; Ilo linali ndi chipulumutso mkati mwake, chipulumutso chinali malo othawirapo.

660 “Kodi ife tikusowa chiani pa chipulumutso?” Anthu lero amati, “Kodi ife sitikukhala pansu pa boma labwino la kachitidwe ka chidemokarase? Nchiani chomwe ife tikusowa?”

661 Ine sindikusamala kachulukidwe ka boma la demokarase lomwe ife tikukhalamo, ife tikusowa Magazi a Yesu Khristu. Kulondola! Ife tikusowa Khristu. Ine ndimayamikira boma la kachitidwe ka chidemokarase; izo ziribe kanthu kochita ndi chipulumutso cha moyo. Mwamtheradi! Maboma amenewo adzatha, ndi fuko lirilonse lidzatha. Ndipo ine ndinaima cha . . . pamene afarao ankaima, ndipo iwe ungachite kukumba mapazi twente pansu pa nthaka kuti upeze mipando yachifumu yawo pamene iwo ankakhala. Afarao onse ndi maufumu ake a padziko lapansi lino, ndipo zinthu zosakhazikika zake zonse zidzalephera ndi kuchokapo, koma Yehova azidzalamulira kwanthawizonse, pakuti Iye ndi Mulungu wachisavundi. Molimba pa thanthwe Khristu Yesu ife tikuima, pakuti maziko ena onse ndi mchenga wotitimira.

662 Sindikusala kaya . . . maufumu aziuka ndi kulephera, koma o, palibe kalikonse . . . Ine sindikusamala kaya ndi . . . chirichonse; palibe chomwe chiripo, palibe chamtsogolo, palibe (njala kapena zowawa kapena chirichonse) zingakhoze konse kutilekanitsa ife kwa chikondi cha Mulungu icho chomwe chiri mwa Khristu. Pamene munthu wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu, iye samakhalanso cholengedwa cha nthawi, koma iye ndi cholengedwa Chamuyaya. Ameni. Iye wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo. Iye wadutsa . . . Iye wadutsa zinthu za nthawi, walowa ku Muyaya. Iye sangakhoze konse kuwonongeka! Ndipo Mulungu analumbira kuti Iye adzamuukitsa iye mu masiku otsiriza.

663 Kotero iwo akhoza kukhala ndi mipingo yanu yonse yaikulu, ndi nthawi zanu zonse zazikulu, ndi zonse mukukhumba

kutero, ndi kumanena nthabwala zanu zoipa ndi kumakhala ndi masewero anu a Bunco, ndi maphwando a supu ndi china chirichonse chimene inu mukufuna kumachita; ndi kukhala naye mlaliki wina wophunzira ataima apo. Mwinamwake iye akhoza kuchita ntchito yabwinoko pa izo kuposa ena a anyamata awa omwe sadziwa nkomwe ma ABC awo. Koma ine ndikukuuzani inu choonadi, ine kulibwino kukhala naye mnyamata yemwe samadziwa ma ABC ake akulalikira kwa ine (yemwe amamudziwa Khristu) kuposa afioroje onse aakulu omwe alipo ndi maphunziro anu onse omwe angakhoze kulingaliridwa. Mwamtheradi!

⁶⁶⁴ Kumusi kuno ku Kentucky, osati kale litali, mnyamata wamng'ono yemwe sankakhoza nkomwe ngakhale kuwerenga dzina lake lomwe, anati Ambuye anamuitana iye kuti azilalikira ndipo ankafuna nyumba ya sukulu. Bwanji, eni ake sakanamuloleza iye kukhala. Mlaliki wina wamkulu wopambana anabwera cha uko ali ndi chogwirizitsa dzina lake monga *choncho*, dotolo wina wamkulu wazamulungu, bwanji, iwo anamulola iye kuti akhale nayo sukuluyo. Zedi. Anali ndi chitsitsimutso cha masabata awiri, popanda moyo umodzi. Ndipo bambo ake anabwerera, anati, “Tsopano inu mwamuloleza uyo kukhala nayo iyo, ine ndimalipira msonkho, ine ndiri ndi ufulu kuti mwana wanga akhale nayo iyo. Ndipo mwana wanga ayenera kuti akhale nayo nayenso.”

⁶⁶⁵ Koteri iye anabwerera kuti akafufuze, ndipo anakawafunsa iwo, iwo anati, “Chabwino, ife timulola iye kuti akhale ndi usiku uwiri wokha.” Ndipo iwo anatero namulola iye kukhala ndi mausiku awiri.

⁶⁶⁶ Ndipo usiku umenewo mnyamata wamng'ono uyo anakafika pamwamba apo ndipo sankakhoza ngakhale kuwerenga Baibulo, anali ndi winawake kuti azimuwerengera nkhani yake. Koma pamene iye anayenda kupita pa nsanjapo, iye anali atadzozedwa ndi Mzimu Woyera. Ndipo pamene iye analalikira, pafupi makumi awiri anabwera ku guwa; ndipo mlaliki wochitazayekha uja analira njira yonse nadutsa mpaka ku Gologota, pa guwa.

⁶⁶⁷ Zedi, m'bale, sindizo—si zomwe iwe umazidziwa, ndi Yemwe iwe umamudziwa. Ndilo lingalirolo, ndi zomwe zimatengera, zimatengera kumudziwa Khristu. Kumudziwa Iye, ndi Moyo; kumukana Iye, ndi imfa.

⁶⁶⁸ Mwamsanga ku mafunso athu ena, tsopano mafunso omwe akupita uko ku Georgia:

67. Kodi miyala mu...imaimira chiani mu Chivumbulutso 21:19 ndi 20?

⁶⁶⁹ Ngati inu mukufuna kuti mutenge nthawi kuti mutsegule mu Mabaibulo anu, chomwe ife tiribe nthawi yochulukira kwambiri tsopano, koma ine ndiyesera kuti ndiwayankhe awa mofulumira.

Chivumbulutso twente- . . . Ine ndikukhulupirira ndi 21:19 ndi 20. Inde.

670 Chabwino, mmenemo inu mupezamo kuti iye anali kuyankhula za miyala yomwe inali mu nyumba. Ndipo miyalayo inali maziko. Ngati inu mungazindikire . . . Ine ndikukhulupirira inu muli nazo izo apo, M'bale Neville. Ndipo mwala uliwonse unali maziko. Osati mwala umodzi maziko, ndi inayo . . . Koma mwala uliwonse unali maziko. Mwala uliwonse unali maziko owirikiza. Ndipo apo panali miyala khumi ndi iwiri. Ndipo ngati inu mungazindikire miyala khumi ndi iwiri iyo, imapereka . . . Poyamba kuyambira ndi jaspi, ndi sardiyo, ndi ina yotero monga choncho, kuimira mwala uliwonse.

671 Mu Baibulo apo inu mupeza kuti iyo inkatchedwa miyala inayake. Ina ya iyo yosiyana pang'ono, inu simunayambe mwamvapo za iyo. Ngati inu mung'ayang'ane mu dikishonare umo inu mupeza kuti ndi mwala womwewo, kungokhala dzina losiyana; litasinthidwa.

672 Koma izo zikuyamba n—ndi yaspi. Yaspi unali mwala w—wa Benjamini . . . kapena mwala wa . . . o, mwana woyamba, Rubeni. Mwala woyamba unali Rubeni, umene unali yaspi. Mwala wotsiriza unali Benjamini, mwala wotsiriza pamwamba.

673 Tsopano, miyala khumi ndi iwiri iyi yomwe maziko anakhazikitsidwapo, iyo—miyala khumi ndi iwiri iyo inkapachikidwa pa chapa chifuwa cha Aroni. Ndipo i—iyo inkaimira, iye anali wansembe wamkulu wa awa—wa mafuko awa. Uliwone wa miyala yawo yakubadwa mkati umu, mu ichi—chotengera ichi. Ndipo pamene anthu ankawona chotengera ichi, iwo ankazindikira kuti Aroni anali wansembe wamkulu wa fuko lonse, pamene iwo ankawona mwala wa kubadwa mu chotengera ichi.

674 Tsopano, pamene ife tinafika mmawa uno mu uthenga wa M'bale Neville. Ndipo nthawizonse zochuluka pamene iwo amabweretsa Urimu Tumimu. Inu mumaziwona izo zikutchulidwa mu Baibulo ngati njira yomwe iwo ankadziwira ngati uthenga wao unali Choonadi kapena ayi. Miyala imeneyo, pamene iwo ankayamba kumanena zomwe munthuyo amanena, mneneri amalosera, ndipo miyala iyo yonse inkanyezimira palimodzi. Iyo inkapanga kuwundana kwa kuwala komwe kumatenga safire, ndi yaspi, ndi kalabankulo, ndi miyala ina yonse iyo kunyezimiritsa kuwala kwawo, iyo inkapanga mtundu umodzi wawukulu wa utawaleza wokongola kwambiri womwe untagwirizanitsa chinthu chonsecho palimodzi.

675 Tsopano, tsopano, lero, pamene Urimu Tumimu iyo inachotsedwa ndi unsembe uja, tsopano Baibulo ili ndi Urimu Tumimu wa Mulungu lero. Ndipo pamene mlaliki alalikira, zisamati zizikhala malo amodzi okha apa, ndipo izo nzonse zomwe iye akuikapo chiyembekezero chake; izo ziyenera

kumakhala Baibulo lonse likunyezimiritsa uthenga umene munthuyo akuulalikira. Icho ndi chinthucho. Osati malo amodzi okha, nkuti, “Chabwino, Baibulo limanena izi.” O, zedi, ilo limanena zinthu zambiri. Koma inu mumayenera kuzipangitsa zonsezo kuikidwa palimodzi. Ndipo pamene Mzimu wa Mulungu ubwera ndi kudzalowa mu—Mawu, Iwo umaziyika izo zonse palimodzi ndi kunyezimiritsa Kuwala kumodzi kwakukulu, ndipo Kuwala kumeneko ndi Yesu Khristu.

⁶⁷⁶ Tsopano, miyala thwelofo iyi inali maziko thwelofo omwe anayambitsidwa kuchokera kwa Rubeni, ndi Gadi, ndi mpaka mmusi kwa Benjamini; mafuko thwelofo, miyala thwelofo. Ndipo miyala iyo mu Kachisi, mu Yerusalemu watsopano Wakumwamba, maziko aliwonse adzaikidwa pa imodzi ya mbadwazo.

⁶⁷⁷ Tsopano penyani, inu muizindikire miyalayo, tsopano inu mukuyenera kuti muzizipenya mbadwa izo zinkanyezimiritsidwa mu chinachakenso, mu funso linalo basi.

68. Tafotokozani—tafotokozani chachinai. . .zirombo zinai za Chivumbulutso 5.

⁶⁷⁸ M'bale Neville, ngati inu muli nazo izo apo pomwe pafupi, kapena ena a inu, pa Chivumbulutso 5, ife tiwerenga izi kwa miniti yokha. N—ndi chithunzi chokongola apa cha. . .Apa, ine ndiri napo ipo mwiniwanga, Chivumbulutso mutu wa 5:

Ndipo ine ndinawona mu dzanja lamanja la iye yemwe anakhala—pa mpandowachifumu bukhu lolembedwa mkati ndi kunja n—n—ndi kumbuyo wake, losindikizidwa ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri.

Ndipo ine. . .

⁶⁷⁹ Tsopano, awo si malo ake. Ine ndikufuna kuti ndifike patsogolo pang'ono, zamoyo zinai. Tiyeni tiwone, ndime ya 14. Chabwino, bwana. Tsopano apa ife tiyeni, ndiko kulondola. Tsopano tiyeni tiyambire pamwamba apa p—pa ndime ya 12, ayi, ine ndikulingalira. . . “Ndipo zirombo zinai zinati, ‘Ameni.’” Ayi, pali malo aang'ono mmbuyo mwa apo, M'bale Neville. “Taonani, ine ndinamva liwu. . .”

⁶⁸⁰ Tiyeni tiwone, miniti yokha, ine ndinali kuziwerenga izo kanthawi kapitako. O, ndi ife apa, tiyeni tiyambire pa ndime ya 6. Ndime ya 5:

Ndipo mmodzi wa aakulu anati kwa ine, Usati ulire: taona, Mkango wa fuko la Yuda, Muzu wa Davide, walakika kuti atsegule bukhu, ndi kumasula. . . zisindikizo zakezo.

Ndipo ine ndinawona, ndipo, . . .mkati mwa mpandowachifumu ndi. . .zirombo zinai, ndi pakati pa akulu, panaima Mwanawankhosa ngati kuti anali ataphedwa, ali ndi mitu isanu ndi iwiri ndi maso asanu

ndi awiri, yomwe ili Mizimu isanu ndi iwiri . . . yomwe inatumiza kuchokera . . . ku dziko lapansi.

681 Ine ndikufuna kuti inu muligwire funso limenelo, ndipo ngati ine sindizigwira izo pansu apa mu miniti, ine ndikufuna kuti inu mulibwerese ilo kachiwiri, ine ndikufuna kuti ndichite pa, “Mizimu isanu ndi iwiri iyo ya maso asanu ndi awiri omwe anali pa Mwanankhosa.” O, ndicho chinthu chokongola kwenikweni. (Chabwino, ife tikufuna kuti titenge funso la m’bale uyu tsopano.) Chabwino, musati muiwale izo tsopano.

Ndipo iye anabwera nadzatenga bukhu kuchokera mdzanja lamanja la iye yemwe anakhala pa mpandowachifumu.

Ndipo pamene iye analitenga ilo, zirombo zinai ndi akulu foro ndi twente anagwa pansu pamaso pa mwanawankhosa, . . . aliynse wa iwo ali ndi azeze, . . .

682 Tsopano, ndizo—zinai—zirombo zinai apa, ngati inu mungazindikire. Tsopano tiyeni tipitirire ndi kuziwerenga izo mopitirira pang’ono pokha:

. . . azeze agolide, . . . odzaza ndi mbale ndi zofukiza, . . . ndi mapemphero a oyera.

Ndipo iwo ankaimba nyimbo yatsopano . . . Ndinu woyenera . . . (ndipo anapitirira napangira zao . . . kupembedza kwawo konse kwa Ambuye)

683 Tsopano, zirombo zinai izi za Chivumbulutso, ngati inu mungazindikire izo, malo aliwonse . . . (Inu owerenga Baibulo, ndi anthu omwe ati akamvetsere ku kujambula kwa tepi iyi). Zirombo zinai izo, zinai ndi nkhope zinai: chimodzi chinali nayo nkhope yonga munthu, chinacho chinali nayo nkhope yonga ng’ombe, ndi nkhope inayo inali yonga mphungu, ndipo nkhope inayo inali yonga mkango. Ndipo sizinali kupita chammbuyo konse, izo sizikanakhoza kupita chammbuyo.

684 Ndi angati akukumbukira bukhu lakale la Chivumbulutso pamene iwo ankaliphunzitsa ilo zaka zapitazo, pamene ine ndinatenga pafupi zaka ziwiri kuno pa Bukhu la Chivumbulutso? Ambiri a nthawi-zakale akukumbukira.

685 Taonani, izo sizikanakhoza kumapita chammbuyo, chifukwa kulikonse komwe izo zinkapita izo zinai kupita chamtsogolo. Ngati izo zinai kupita njira *iyi*, izo zinkapita ngati munthu; ngati izo zinkapita njira *iyi*, izo zinkapita ngati mkango; zikamapita njira *iyi*, izo zinkapita ngati mphungu; ngati izo zinkapita njira *iyi*, izo zinkapita ngati ng’ombe. Mwaona, izo sizikanakhoza kumapita chammbuyo, izo zinai kupita chamtsogolo nthawizonse.

686 Tsopano zirombo zinai izo. Tsopano mwamsanga kuti timvetse izi, chifukwa ine sindikufuna kuti ndikhale motalikitsa kwambiri pa izi. Koma zirombo zinai . . . *Chirombo*, mu Baibulo,

chimaimira “mphamvu.” Ndipo inu zindikirani kuti zirombo izi sizinali kutali uko mu dziwe kapena mnyanja kwinakwake zikutuluka kunja koma izo zinali ku Mpandowachifumu wa Mulungu ndipo zinali kumupembedza Mulungu. Zirombo zinai izo zikutanthauza mphamvu zinai zomwe zikuchokera pa dziko lapansi, ndipo mphamvu zinai izo zinali Mauthenga anai: Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane; imodzi simatsutsana ndi imzake.

⁶⁸⁷ Ndipo mmodzi wa iwo, a... Pamene Uthenga ukupita apo ngati mkango, ndi wokaka, ndi wolimba; Uthenga ndi wolimbantima ngati mkango, ndipo iwo ndi mfumu monga mkango. Ngati iwo upita cha ku nkhope ya munthu, iwo ndi wokanika ndi wochenjera monga munthu. Ngati iwo ukupita ngati mphungu, iwo umakhala ndi mapiko aliwiro mu utali wokwera. Izo... Mukuona zomwe ine ndikutanthauza? Ngati iwo ukupita ngati ng’ombe, ndi kavalo wantchito yemwe angakhoze kukoka, ng’ombe ya ntchito yomwe imakoka k—k—katundu wa Uthenga. Zirombo zinai zinali mphamvu zinai, zomwe zinali... Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane; Mauthenga anai amene akumvekera mu Kukhalapo kwa Mulungu. Uwo unali...

⁶⁸⁸ Ngati inu mungazindikire, izo zinali ndi maso kutsogolo ndi kumbuyo. I—izo... Kulikonse komwe izo zinkapita, izo zinkanyezimiritsa. Izo zinkawona kulikonse komwe izo zinali kupita. Ndipo iyo ndi mphamvu ya Mauthenga pamene iwo ukupita kwina, iwo ukhoza... Iwo uli ndi kuchenjera kwa munthu; iwo uli ndi liwiro la mphungu; iwo uli ndi—m—m—mphamvu, mphamvu yokokera, chonyamula katundu ngati ng’ombe; izo ziri nako k—kukaka ndi kulimbantima kwa mkango. Mwaona, ndi Mauthenga anai, omwe ali mphamvu zinai za Chivumbulutso, mutu wa 4.

Chabwino, tsopano lotsatira:

69. Kodi akulu twente ndi foro ndi ndani? Chabwino, ine ndikukhulupirira izo zingakhale ziri pa—a... **Kodi akulu twente-foro ndi ndani?**

⁶⁸⁹ Tsopano izo ndi zophweka basi, ife tikhoza kufika kwa izo. Akulu twente foro omwe amakhala patsogolo pa Mpandowachifumu. Ndi mu... ine ndikukhulupirira ndi mu ndime 4, pamene izo zikupezeka. “Ndipo apo panatuluka china...” Ine ndapeza pa... Tiyeni tiwone, ine ndiri pa... 4:10.

⁶⁹⁰ Chabwino, Chivumbulutso, mutu wa 4, ndi ndime ya 10. Ndiko kulondola. Ife tifika kwa izo.

Ndipo akulu foro ndi twente anagwa pamaso pa iye yemwe anakhala pa mpandowachifumu, ndipo anamupembedza iye yemwe alimoyo kwa nthawi

za nthawi, ndipo anaponyera nduwira zawo ku mpandowachifumu ndi kumati,

Ndinu woyenera, O Ambuye, kuti mulandire ulemerero ndi ulemu ndi mphamvu: pakuti inu munalenga zinthu zonse, ndipo mwa kukondweretsedwa kwanu izo zilipo ndipo zinalengedwa.

⁶⁹¹ Tsopano akulu foro ndi twente. Mkulu ndi woyang'anira zonse. Tsopano zindikirani, iwo anali mbadwa thwelofu ndi atumwi thwelofu. Ndipo iwo anali atakhala, thwelofu kumbali imodzi ndi thwelofu ku inayo. Panali akulu twente ndi foro, omwe anali: mbadwa thwelofu kumbali imodzi, Chipangano Chakale; atumwi thwelofu kumbali inayo, a Chipangano Chatsopano. Kodi Yesu sanati, “Inu mudzakakhala pa mipandoyachifumu thwelofu, mukuweruza mafuko thwelofu a Israeli?”

⁶⁹² Ndi tsopano mazikowo. Taonani, muli ngakhale mtengo mmenemo. Ndipo mtengo kumbali iliyonseyo umabala zipatso za mitundu thwelofu. Ndipo iwo amakolola zipatso zawo kamodzi pa mwezi, yomwe ili miyezi thwelofu pa chaka. Iyo inkapereka mitundu thwelofu ya zipatso chaka chirichonse pamene icho chikupitirira. Thwelofu, mwa chiwerengero cha “kupembedza,” inu mukuona. Ndipo pali twente ndi foro, omwe akanakhala twente-foro, atumwi thwelofu ndi mbadwa thwelofu. Iwo akukhala ku Mpandowachifumu.

⁶⁹³ Chabwino, tsopano ndime ya 4 . . . kapena funso lachinai:

70. Kodi chingwe chofiira mu Genesis 38 chinkaimira chiani?

⁶⁹⁴ Chingwe chofiira, ngati inu mungazindikire, icho chinali Yuda. Ndipo iye anali ndi ana, ndipo mmodzi wa ana ake aamuna anakwatira mkazi wa Chikanani. Ndipo mkazi wa Chikanani uyu analibe ana aliwonse, ndipo mwana wakeyo anafa. Ndiye, lamulo ndiye linali loti atenge . . . mwana wotsatira ankayenera kuti amutenge mkazi wa m'bale wakeyo, ndi kuutsira mbewu kwa wakufayo. Ndipo mwamuna winayo sanachite mwamgwirizano ndi kuchita momwe iye akadayenera kuchita, ndipo Ambuye anamupha iye. Ndiye iye anali ndi mwana wina wamng'ono; chotero Yuda anati, “Dikira mpaka mwana uyu atayenda . . . atakula kufika pa malo pomwe iwe ungasakwatiwe naye.”

⁶⁹⁵ Ndipo pamene iye anakula kufika pa malo omwe iye ankayenera kuti akwatire mkazi wakale wa abale ake awiriwo, chabwino, iye ankayenera kuti amutenge iye apo, kuti awutsire mbewu kwa abale ake omwe anali ata . . . omwe anali atafa asanadzepo iye. Yuda sanamupatse mkaziyo (mkazi wa Chikanani) mwana, mnyamata uyo, ndipo amangomulola iye azipitirira. Kotero iye anawona kuti iye anali kuchita zolakwika,

kotero iye anapita kunja nakazikulunga chophimba pa nkhope yake, ndi kukhala pamalo apagulu momwe hule akanakhallira.

⁶⁹⁶ Yuda anadzera apo ndipo anamutenga mkaziyo ngati mkazi wake, ndipo iye anali hule, ndipo anakhala ndi iye. Ndipo anati, iye anati, “Chabwino, kodi iwe ungandilonjeze chiani ine?” Ndipo iye. . . iye anati. . .

⁶⁹⁷ Iye anati, “Ine ndimupatsa iye—mwana wambuzi.” Iye anati, “Chabwino, ndipatse ine chizindikiro kuti iwe udzachita izo.” Kotero iye anatenga ndodo yake ndi mphete yake ndi zina zotero, ndipo anazisunga izo.

⁶⁹⁸ Ndipo pamene iye anamubweretsa mwana wambuziyo, iwo sanakhoze kumupeza huleyo, chifukwa iye sanali hule.

⁶⁹⁹ Patapita kanthawi, iye anawonekera kuti iye anali woti akhala mayi. Ndipo pamene iye anasonyeza kuti iye anali woti akhala mayi, iwo anabwera nadzamuza Yuda. “Mpongozi wanu wamkazi wachita za uhule.” Anati, “Chifukwa kuti i—iye ndi woti akhala mayi, ndipo anyamata anu onse anafa.”

⁷⁰⁰ Iye anati, “Chabwino, iye aitanidwe pakali pano, ndi kumuwocha iye.”

⁷⁰¹ Ndipo kotero iye anatumiza mawu kwa Yuda, ndipo iye anati, “Mwamuna yemwe anachita izi, ndi mwini wa ndodo iyi ndi mphete iyi.” Chabwino, awo anali apongozi-ake-aamuna.

⁷⁰² Ndipo iye anati, “Iye ndi wolungama kwambiri kuposa momwe ine ndiriri.”

⁷⁰³ Tsopano, pamene iye anadziwa kuti mwana wake anali woti abalidwe, iwo anali mapasasa. Ndipo pamene mapasawo. . . Mwana woyamba yemwe anali woti abadwe, mwambo wakale wa Chiyuda, mwana woyambayo amakhala ndi ufulu wakubadwa, mwana woyamba kutulukirapo. Ndipo uyo, kumbukirani, anali mwana wake woyamba. Palibe wina wa anyamatawo anali ndi mwana naye. Iye anali asanakhale ndi mwana kufikira nthawi iyi.

⁷⁰⁴ Ndipo pamene mwana wake woyamba anatulukira apo, ilo linali dzanja lokha. Ndipo anamwino anaika chingwe chofiira pa dzanjalo, chifukwa chingwe chofiira chinkayankhula za chiwombolo chomwe mwana woyamba wa namwali Maria akanadzakhala. . . anali ndi chingwe chofiira cha chiwombolo.

⁷⁰⁵ Ndipo pamene iye anakokera mkati dzanja lake, winayo anabwera moyambirira. Ndipo pamene iye anatero, anati, “Nchifukwa chiani iwe wachita izi? Winayo ndi yemwe ali ndi ufulu wa kubadwa.”

⁷⁰⁶ Chotero ndi chimene Genesis 38 akutanthauza, inu mukuona. Kutu mwana woyambayo akhalabe ali mpaka pa kudza kwa Ambuye Yesu Khristu. Kutu woyambayo anali pansu pa lamulo la kuombola.

⁷⁰⁷ Inu mukudziwa ine ndinati...bulu wamng'ono, inu mukudziwa, ine ndinakuuzani inu za iye, kuti maso ake anali...chirichonse chowonjezerapo, makutu ake anali ogwera pansi, koma, ngati iye anabadwa ndi ufulu wakubadwa, mwanawankhosa wosalakwa, wamngwiro anafa m'malo ake. Ndi izo apo.

⁷⁰⁸ Kotero izo zinali kwa ufulu wakubadwa. Mwana woyamba yemwe anatulukira kuchokera kwa amake, ndipo iwo analiwona dzanja limenelo (ndipo iwo anadziwa kuti ilo likanakhoza kubwerera kachiwiri). Ndipo pamene iye anakankhira dzanja lake apo kuti asonyeze kuti iye anali nawo iwo, iye anali woyambayo, anamwino anamumanga chingwe chofiira kuzungulira ilo ndipo iye anakokera dzanja lake mmbuyo. Mwaona? Koma, mwamtheradi, iye anali woyamba. Icho chinali chingwe chofiira, chingwe chofiira chakhala... njira yonse kudutsa mu Baibulo, icho chimatanthauza chiwombolo; chomwe chinkalozera mtsogolo kwa mwana woyamba amadzayo.

⁷⁰⁹ Kavalo woyamba kubadwa, ng'ombe woyamba kubadwa, chirichonse chomwe chinali, chirichonse chomwe chinabadwa moyambirira (chomwe chinatulukirapo) chinali pansi pa chiwombolo, chinkayenera kuti chiwomboledwe; chirichonse chinkayenera kuti chiwomboledwe! Aleluya! O, izo zimangondikondoweza ine. Kodi inu mukuzimvetsa izo? Woyamba ankayenera kuti aziwomboledwa. Ilo linali lamulo. Lodala likhale Dzina la Ambuye!

⁷¹⁰ Ndipo pamene Yesu Khristu anabadwa, Iye analiwombola dziko lonse. Ndithudi, Iye anatero. Iye anali Muomboli wa cholengedwa chirichonse chomwe chinayamba chalengedwapo pa dziko lapansi. Iye anali Muomboli. Ndipo pa...chiwombolo chonse chiri mwa Iye, ndipo palibe njira ina konse yomwe inu mungabwerere konse ndi ntchito zabwino, pa kujowina mpingo, kapena chirichonse chomwe chiri; inu mumayenera kubwera ndi chingwe chofiira icho, Muomboli uyo, Muombolo wapachibale uyo.

Chabwino, tsopano lotsatira ndilo:

71. Kodi mphatso ziri kuti...Kodi mphatsozo ndi chiani zomwe zizidzatumizidwa molingana ndi imfa ya mboni ziwiri, za Chivumbulutso 11?

O M'bale Palmer, ngati inu simungakhoze kufunsa mafunso ena!

⁷¹¹ Tsopano, chiwombolo, zingwe izi apa, chingwe chofiira ichi, ife tikuchiwona chinkatanthauza chiwombolo.

⁷¹² Tsopano funso lotsatira ndilo:

Mphatsozo ndi chiani mu Chivumbulutso 11?

713 Ikubwera nthawi...Tsopano pano tikuti tiyankhe funso lomwe linayankhidwa usiku wina, lomwe mlaliki mzanga wa ine analemba lokhudza Ayuda, momwe izo ziti zidzakhali.

714 Tsopano Ayuda awa ali ndi zaka zitatu ndi theka zolonjezedwa kwa iwo. Ndi angati amadziwa zimenezo? Masabata sevente analonjezedwa. Anati, “Mesiya adzabwera ndipo adzadulidwa pakati.” Zaka zitatu ndi theka Khristu analalikira, anaphedwa ndendende mu zaka zitatu ndi theka, zaka zitatu ndi miyezi isanu ndi umodzi Iye analalikira.

715 Ndiyeno themberero lopangitsa chipululutso, chi—chisilamu cha Omar chinaikidwa pa Malo Oyera; monga Mulungu ananena, zaka twente faifi handiredi izo zisanachitike, iwo ukanadzakhala utaima apo. Mneneri anaziwona izo, ndipo anawuona iwo, ndipo anati, “Iwo akanadza...Amitundu akanadzakhala eni ake a apo mpaka nyengo ya Amitundu itatsirizidwa.”

716 Tsopano zikadalipobe zaka zitatu ndi theka zolonjezedwa. Ngati inu mungazindikire, mboni izi za Chivumbulutso 11 zinalosera masiku sauzande, thuu handiredi ndi sikisite; ndendende zaka zitatu ndi theka. Tsopano...ndipo iwo anali atavala ziguduli. Tsopano, penyani utumiki wao, chomwe iwo ali. Tsopano, mboni ziwiri izi zaphedwa.

717 Tsopano, a...Iwo anabwerera kwa Ayuda utachitika Mkwatulo wa Mpingo wa Amitundu. Mpingo wa Amitundu ukupita Kwawo ku mgonero wa chikwati, ndipo monga Rebeka anatengedwera ku malo a Abrahamu ndi Isaki ndipo uko anakakwatitsidwa. Ndipo Rebeka ndi Isaki anatuluka natenga kwathunthu chirichnse chomwe Abrahamu anali nacho, izo zonse zinapita kwa Isaki. Mwamtheradi! Ndipo izo sizikanakhoza kubwera kwa Isaki mpaka poyamba Isaki atakwatira. O Aleluya! Ndi inu apo.

718 Ndipo Khristu kukhala...Mulungu ankakhala mu thupi langwiro, lowonongedwa kwathunthu kwanthawizonse lija ndi kudutsa mu Muyaya. Pamene Mwanawankhosa ndi Mkwatibwi akwatirana Kumwamba, iye akuyenda mwa umwini wathunthu. Mwamtheradi! Isaki ndi Rabeka anabwera apo mwa umwini wathunthu.

719 Ndipo pamene mwambo uwu uli kuchitika Kumwamba, wa Mkwatibwi, Mkwatibwi wa Amitundu ali kukwatitsidwa kwa Kalonga (Mwana wa Mulungu), mu Ulemerero; pamene iwo ali kukwatitsidwa, pali zaka zitatu ndi theka zoti zichitike pamene...Mose ndi Eliya...

720 Chomwe, Mose sanasowe konse...ayi, thupi lake linanyamulidwira kwina. Angelo anamutenga iye, iye sanavunde, iye sanaonongeke. Iye anali choimira changwiro cha Khristu. Iye anafa ndipo Angelo anamunyamula napita naye, ndipo ngakhale Mdierekezi sadziwa konse komwe iye anaikidwa,

ndipo anayesera kukangana ndi Mikaeli Mngelo wamkulu za kuikidwa mmanda kwake. Ndi chomwe Baibulo limanena. Mulungu anamutengera iye mmwamba mu mkwatulo.

⁷²¹ Ndipo Eliya, pamene iye anali akuyenda uko, mneneri wa Mulungu, anayenda kupita ku Yordani, anavula mkanjo wake ndipo anakantha madzi, ndipo iwo anagawikanira kumanja ndi kumanzere. Iye anayenda nakwera phiri. Elisa anati. . . Anati, “Kodi iwe ukunditsatira ine chiani?”

⁷²² Iye anati, “Ine ndikufuna magawo awiri a Mzimu wanu.”

⁷²³ Anati, “Iwe wafunsa chinthu chovuta, koma ngati iwe undiwona ine pamene ine ndizipita.” Iye anasunga maso ake pa iye.

⁷²⁴ Ndipo patapita kanthawi, kutsika kuchokera Kumwamba kunadza galeta wa moto ndi Angelo a moto, akavalo a moto, ndipo Eliya anakwera apo ndipo anapita mmwamba ku Ulemerero. Iye sanalawe konse imfa, iye anasinthidwa, iye ayenera kuti afe!

⁷²⁵ Ndipo ngati inu muti muwapenye aneneri awiri awa a Chivumbulutso 11, iwo akuchita chinthu chomwechomwecho chimene Mose ndi Eliya anachita. Inu mukuti, “M’bale Branham, kodi inu mukutanthauza kuti mudiuze ine kuti Eliya ndi Mose akadali moyo?” Mwamtheradi!

⁷²⁶ Bwanji, chisanachitike Chiwalitsiro cha pa Phiri. . . Pa Phiri la Chiwalitsiro, Yesu asanapite ku Kalvare, apo anaima onse Mose ndi Eliya ataima apo akuyankhula kwa Iye. Ndithudi, iwo anaterodi, iwo sanafe. Ndipo iwo sanafe konse; iwo ndi zivundi, iwo ayenera kuti adzafe. Chotero iwo angokhala mu chikhalidwe chaulemerero akuyembekezera nthawi imeneyo.

⁷²⁷ Ndiyeno pamene iwo abwerera ndi kudzalalikira ndendende zaka zitatu ndi theka pansi pa kudzoza kwa Ubatizo wa Mzimu Woyera, pamene madalitso achotsedwa kwa Amitundu (ndipo Mpingo watengedwera mmwamba); ndipo mpingo wozizira, wachizolowezi ukusakidwa ngati agaru, ndi achikomisini ndi gulu la Chiroma, ndipo pamene iwo asakidwa ndi kuphedwa. I—iwo adzaphedwa apono; aneneri awa atalalikira zaka zitatu ndi theka, ndipo Baibulo linanena kuti iwo anaphedwa mu waukulu. . . mu msewu, wotchedwa mwauzimu, Sodomu ndi Igupto, kumene Ambuye wathu anapachikidwako. Umo ndi mu Yerusalemu mommuja; mwaona, mu Yerusalemu mommuja, motchedwa mwauzimu.

⁷²⁸ Ndipo iwo anagona pa msewu kwa masiku atatu ndi usiku. Ndiyeno pa kutha kwa masiku atatu ndi theka, mzimu wa moyo unabwera mwa iwo ndipo iwo anaukapo. Iwo anayenera kuti afe monga zivundi zina, iwo anayenera kuti atero. Ndipo pamene iwo anawapha alaliki awiri awa. . .

729 Iwo anali atalalikira motsutsa zolakwika, ndipo iwo anatsitsa moto kuchokera kumwamba. Nndani anachita zimenezo? Mwaona? Iwo anatsitsa miliri kuchokera kumwamba, ndipo analikantha dziko mofulumira monga... ndi pa nthawi iliyonse yomwe iwo anafuna kutero. Ndipo iwo anatsitsa moto kuchokera kumwamba. Ndipo iwo anaimitsa miyamba kuti isavumbe, utali wa momwe iwo ankafunira kutero. Anali ndani amenewo? Ndendende Mose ndi Eliya. Ndi izo apo mboni ziwirizo.

730 Ndipo pamene iwo anawuzunza mpingo, kapena dziko, ndi kulalikira kwawo; ndi kuwalandiranso Ayuda, ndi kuwabweretsanso iwo ku kulapa, kuwabweretsanso iwo ku kukhulupirira apo... Pamene iwo amuwona Yesu akudzera Mkwatibwi, iwo adzati, "Taonani, uyu ndi Mulungu wathu yemwe ife tinali kumuyembekezera. Ndi Iyeyu!" Koma Iye sakuwadzera iwo; Iye akubwera kudzatenga Mkwatibwi Wake. Ndipo Mkwatibwi Wake...

731 Pamene Yosefe anapita ku Igupto, iye sanawatenge abale ake limodzi naye, koma iye anapeza mkwatibwi wake kumeneko. Mwamtheradi! Koma pamene iye anadzidziwitsa yekha kwa abale ake, uko kunalibe aliyense pamenepo. Ndizo ndendende kulondola. Ndipo pamene Iye azidzipangitsa Iyeyekha kudziwika kwa Ayuda awa, sipadzakhala wina aliyense apo koma Ayuda. Awo ndi omwe anamupha Yosefe, ataima apo; ndipo iye anati, "Chabwino, ndine Yosefe, m'bale wanu." Ndipo iye analira.

732 Ndipo iwo anati, "Tsopano ife tikudziwa ife talowamo, chifukwa ife tinamupha iye."

733 Chinthu chomwecho, Ayuda awo adzakhala nayo nthawi yaikulu iyo ya vuto kudza kusanachitike kumene tsopano, kwa chisautso chowathamangitsira iwo kuti abwerere ku dziko la kwawo. Kuwaingitsa iwo ngati gulu la nkhosha zikubwerera kuchokera ku Phiri la Kalimeri kutali.

734 Pamene Ambuye Yesu azidzadzera Mkwatibwi wake, ndipo iwo akadzamuwona Iye, iwo adzati, "Uyo ndi Yemwe ife tinali kumuyembekezera, ndi Uyo apo!" Iye adzauka ndi machiritso mu mapiko Ake. Ndiko kulondola.

735 Ndipo mpingo, otsalira a Ayuda, pamene iwo potsiriza ati adzawapha aneneri awiri awa, ndipo iwo nkudzagonekedwa mu msewu wotchedwa mwauzimu Sodomu ndi Igupto, kumene Ambuye wathu anapachikidwako, iwo azidzatumizirana mphatso kwa wina ndi mzake (dziko lizidzatero).

736 Tsopano, M'bale Palmer, ndi apano inu. Yang'anani mmbuyo ku mbiriyakale ya Chiroma ndipo inu mukapeza kuti kuli fuko limodzi lokha mu dziko lonse lomwe linkatumiza konse mphatso itatha nkondo, ndiwo Ufumu wa Chiroma.

737 Ndi chifukwa chake ine ndimanena kuti wotsutsakhristu achokera ku Roma. Chirombo chochokera ku Roma, icho sicingakhoze kuchokera ku Moscow. Ichu chichokera ku Roma, chinjoka chofiira chomwe chinaima pa mkazi kuti chimulikhwire mwanayo mwamsanga pamene iye anabadwa. Mdierekezi uyo, anali kuti mdierekezi ameneyo? Anali ndani iye? Kaisara Augustus yemwe anawatuma kuti akaphe ana onse oyambira usinkhu wa zaka ziwiri kutsika. Chinjoka chofiira, chinjoka, *chirombo* chimatanthauza “mphamvu.” Mphamvu ya Chiroma inazunza ndi kuyesera kuti amupeze Khristu Mwana uja.

738 Ndipo chinthu chomwecho! Nthawi iliyonse yomwe Aroma, Aroma akale achikunja ankakhala ndi chigonjetso chachikulu, iwo ankakhoza kumatumiza miyala yoyera ndi chirichonse kwa wina ndi mzake, ngati mphatso monga choncho, ngati chikumbutso. Chotero miyala iyo yomwe inali. . . Chomwe iyo inali, inali mphatso zazing’ono zotumizidwa pakati pa a mu mpingo wa Chiroma. Mwamtheradi! Ndendende. Izo ziyenera kukhala ziri.

739 Ine ndinaima apo pomwe mu Mzinda wa Vatikani ndipo ndinazitsimikizira izo ndi Baibulo. Papa atavala nduwira yapatatu, *Vicarius Fili Dei*, zinthu zonse izo zomwe ine ndinazimva ndi zina zotero, ndi za mwamtheradi choonadi; gulu lachipembedzo lomwe limalamulira fuko lililonse la pansi pa Kumwamba, ndipo ilo limatero. Ndi izo apo, ziri choncho.

740 Palibe chotsutsana nawo anthu Achikatolika (ayi, bwana), iwo ali abwino basi monga wina aliyense, koma chipembedzo chawo ndi cholakwika malingana ndi Baibulo ili. Ngati Baibulo ili likulondola, iwo akulakwitsa. Iwo amati iwo sama. . . “Ziribe kanthu chomwe Baibulo limanena, ndi chomwe mpingo unena.” Ife timakhulupirira kuti Baibulo limayankhula ndi ulamuliro wapamwamba! Mwamtheradi, ndi Mawu a Mulungu.

741 Kotero inu mukuona apo, miyala iyi yomwe inkatumizidwa apo, ya mu Chivumbulutso apa, ndi—miyala yomwe inali mphatso zinkatumizidwa kwa wina ndi mzake. Chomwe chimangosonyeza kuti. . . Baibulo linati, Mu chivumbulutso apa, amati, “Mulole iye amene ali ndi nzeru awerengere chiwerengero cha chirombo. Mulole iye yemwe ali ndi nzeru achite *zakuti-n-zakuti*. Mulole iye yemwe ali ndi mzimu wa mphatso zinazake achite *mwakuti-n-mwakuti*.” Inu mukuona momwe mpingo uliri woprewera?

742 Mnyamata amandifunsa ine mmawa uno pa za mphatso zauzimu, pa za kuyankhula ndi malirime. Mnyamata wamng’ono, wodzipereka kwambiri, ine ndikukhulupirira iye ndi woti adzakhale mtumiki masiku ena awa. Ndipo pa za mpingo, ine ndinati, “Pali zochulukwa kwambiri za izo zomwe

ziri zathupi. Ife sitikufuna izo, koma ife tikufuna chinthu chenicheni. Ife tikukhumba titakhala nazo izo.”

⁷⁴³ Inu simungakhoze kupita kumakaphunzitsa izo mu mpingo; chinthu choyamba inu mukudziwa, inu mumapeza, wina ali ndi lirime, wina ali ndi salimo, ndiye iwe umayenera kuti umenyane nacho chinthucho apo. Koma pamene Mulungu apereka mphatso mwayekha, iyo imadziwonetsera payokha. Ndiko kulondola. Mwaona, ndiyo mphatso ya Mulungu, ndiyo imene Iye amaitumiza kwa Mpingo kuti ugonjetsere.

⁷⁴⁴ Tsopano, wotsutsakhristu ali ndi chinachake chonga chofanana ndi chosiyana, icho chiri ndi—n—njira yopotozedwa yochitira izo. Ndipo uwo ndi ufumu wa Chiroma umene amatumiza mphatso kwa wina ndi mzake, mphatso zachilengedwe. Mulungu amatumiza mphatso zauzimu kwa ogonjetsa; Aroma amatumiza mphatso zachilengedwe kwa wina ndi mzake.

⁷⁴⁵ Ife tikukhulupirira kuti Mzimu Woyera ndi Mzimu, ife timawulandira Iwo mwa ubatizo umene umachokera Mmwamba.

⁷⁴⁶ Mpingo wa Katolika umaphunzitsa, “Ukarisitiya woyera womwe uli thupi la Khristu; kuti pamene iwe uwulandira mkate uwu ndi woyeretsedwa, iwo ndi Mzimu Woyera, Mzimu Woyera, ukarisitiya woyera.” Mwaona?

⁷⁴⁷ Ife timakhulupirira kuti ndi chidutswa cha mkate, ife sitimakhulupirira kuti ndi thupi la Khristu, (ife tikukonzera kuti titenge izo mu maminiti pang’ono). Ife timakhulupirira kuti iwo umaimira thupi la Khristu. Koma ilo si . . .

⁷⁴⁸ Ndiko kusiyana kwa pakati pa chiphunzitso cha Chikatolika ndi Chiprotestanti. Mukuona? Mpingo wa Katolika umati, “Thupi ndilo . . . Mkatewo *ndi* thupi lenileni. Mpingo uli nayo mphamvu yousinthira iwo.” Kodi inu munayamba mwamuwona Mkatolika akamadutsa pa tchalitchi, amaweramitsa mutu wake, amapanga mitanda? Ndi chifukwa cha kuwala kwakung’ono uko kumayaka mu mpingo umoko pansu pa kachisi wamng’ono uyo. Ali ndi kuwala kwapang’ono mmenemo, ndi mkate woyeretsedwa uwo uli mmenemo. “Ndipo ilo ndi thupi la Khristu. Ndipo pamene iwe udyia izo, iwe mwamtheradi umakhala ukudya thupi lenileni la Khristu pa mgonero wako woyamba ndi kuvomereza kwako ndi zina zotero. Iwe ukudya, kwenikweni, thupi la Khristu.”

⁷⁴⁹ Ife timanena kuti iwo *umaimira* thupi la Khristu, mwaona, kuti iwo si kanthu mu dziko koma chidutswa cha mkate. Ndipo ziribe kanthu ngati iwo ukanati usakhale mkate nkomwe, ngati iwo ukanakhala china chirichonse, iwo ukanati uzimimira chimodzimidzi basi. Basi—basi ndendende. Kaya iwo . . .

⁷⁵⁰ Monga anthu awa omwe amati, “Ine sindingati ndibatizidwe mu dziwe, ine ndikufuna kuti ndidzakabatizidwe mu mtsinje.”

⁷⁵¹ Kodi izo zimapangitsa kusiyana kotani, bola ngati iwe wabatizidwa? Ngati liri dziwe, ndi. . .Bwanji, Filipino anabatiza mu dziwe. . .pamene mdindo anabatizidwa. Pamene Filipino anamubatiza mdindo mu dziwe, Mzimu Woyera unamukwatula iye mochuluka kwambiri kuti Iye anamutengera Filipino kutali, iye sanawoneke kwa mailosi mazana awiri. Anamutengera Iye mu Mzimu, anamupatsa iye—galeta wochokera Kumwamba komwe kwa mazana awiri. Amen. Zodabwitsa!

Tsopano:

Kodi oyera adzakakhala ali kuti ukadzatha ulamuliro wa zaka chikwi chimodzi? Ndipo kodi ndi thupi la mtundu wanji lomwe iwo ati adzakhale ali nalo? Ine ndibwerera ku izo mu kamphindi [M'bale Branham akuyankha izi kuyambira pa ndime 820, ngati funso 74—Mkonzi]. Iwo adzakakhala ali ndi Yesu.

⁷⁵² Chabwino, f—funso la chisanu ndi chiwiri:

72. Kodi tidzawaweruza chotani angelo?

⁷⁵³ Izo zikupezeka mu. . .Kodi ife tidzawaweruza chotani angelo? Pokhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Angelo ndi antchito; ife ndi ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Ndipo Baibulo linanena kuti ife tidzawaweruza angelo. Ndiko kulondola. Tsopano, tsopano ngati inu. . .

Ndi funso lachisanu ndi chitatu:

73. Nchiani tsitsi chifukwa cha angelo pa I Akorinto?

⁷⁵⁴ Tsopano winawake andipezere ine I Akorinto, m—mutu wa 11, ndipo ife tiwona apo, kuti inu mupeza k—kuti. . .Mu I Akorinto, w—wa 11, ife tinapezapo kuti Paulo akuyankhula. Ndiroleni ine ndifike kwa izo miniti yokha, ndiyeno ife tiziwerenga izo mofulumira ndithu ndiyeno ife ti—ife tikhala nazo izo pansu.

⁷⁵⁵ Ine ndiri ndi chinachake choti ndinene pa ndime ina iyi apa, yomwe ine ndikuyembekeza Ambuye ayipereka iyo kwa ife momwe ife tikuyenera kukhalira nayo iyo. Ngati winawake angaipeze iyo. . .Ine ndikuganiza iwo ndi mutu wa 11, eya, chabwino. Tsopano mvetserani mwatcheru, mwatcheru kwenikweni tsopano, chotero kuti inu mumvetse. Tsopano tengani chikumbumtima chanu chonse ndi kuchiika icho mu thumba lanu la bulandi mpaka ine nditsirize kuwerenga izi, inu mukuona, kuchitira ndemanga pa Izo. Mvetserani mwatcheru kwenikweni, izi ndi PAKUTI ATERO AMBUYE:

Khalani inu onditsatira ine, ngakhale monga ine. . . ndiri wa Khristu. (Paulo anati, “Inu zinditsatirani ine, monga momwe ine ndikutsatira Khristu.”)

Tsopano ine ndikukuyamikani inu, abale, kuti inu mumandikumbukira ine mu zinthu zonse, ndi kusungu

*kwa malangizo, monga ine ndinawaperekera iwo...
kwa inu.*

*Koma ine ndikanafuna inu kuti mudziwe, kuti mutu
wa mwamuna aliyense ndi Khristu; ndipo mutu wa
mkazi ndi mwamuna; ndipo mutu wa Khristu ndi
Mulungu.*

756 Mukuona momwe izo ziliri? Mulungu, Khristu, mwamuna,
mkazi. Tsopano:

*Mwamuna aliyense wopemphera kapena kunenera, ali
ndi mutu wake wophimbidwa, amanyozetsa Khristu.*

*Koma mkazi aliyense wopemphera kapena kunenera
mutu wake usanaphimbidwe amanyozetsa mutu
wake:...*

757 Tsopano ife titenga izi miniti yokha, ndi kukusonyezani inu
kuti tsitsi kwa mkazi ndi chophimba chake:

*...pakuti izo...ngakhaletu zonse ziri chimodzi ngati
kuti iye anali atametedwa. (izo zikutanthauza kuti n—
ngati iye ati adule tsitsi lake, ndiye limetedwe ilo lonse)*

*Pakuti ngati mkazi akhala wosaphimbidwa,
mumulole iye aponso asengedwe: (asengedwe
amatanthauza ametedwe, mwaona)...koma ngati
chiri chamanyazi kwa mkazi kuti akhale atasengedwa
kapena kumetedwa, msiyeni iye akhale wophimbidwa.*

758 Tsopano ife tikufika kumene ku funso lomwe mukufunsalo.
Mwaona? Chabwino, tsopano ndi zolakwika kuti—dona adule
tsitsi lake, molingana ndi Baibulo. Tsopano inu mveterani apa
pomwe ndi kumuwona ngati Baibulo silimamupatsa mwamuna
ulamuliro wovemerezeka kuti amuchotse mkazi wake ngati iye
adula tsitsi lake, onani, ngati izi ziri zolondola kapena ayi.

*Ngati mwamuna...Pakuti mwamuna indedi sayenera
kuti aziphimba mutu wake (uko, ndiko kukhala ndi
tsitsi lalitali), pakuti ndi mochulukwa momwe iye ali
mu chifanizo ndi ulemerero wa Mulungu. koma mkazi
ali mu ulemerero wa mwamuna. (kodi inu munayamba
mwaganizapo izo?)*

759 Tsopano ine ndikufuna kuti ndiime apa, chifukwa ine
ndikufuna izi kuti zilowerere mkati bwino kwenikweni,
mwaona. Ndipo tsopano kumbukirani, ine ndawonapo makumi a
zikwi za akazi okondeka (ndikuwadziwa iwo pakali pano, ndipo
ochulukwa a iwo akhala mu mpingo muno) omwe ali ndi tsitsi
lalifupi, omwe ali Akhristu. Ndipo chomwe ine ndikuyikirapo
izo si inu, ndi momwe inu munaphunzitsidwira. Mwaona?
Ndi zimenezo. Mlaliki wanu sanakuuzeni konse inu izi. Koma
ngati wina aliyense wa akazi ozungulira pa Kachisiyu monga
choncho, ndiye iwo ndi olakwa. Mwaona, chifukwa ife ndithudi
timawauza iwo za izo.

760 Tsopano, tsopano penyani izi:

...mwamuna...Pakuti... (ndime ya 7)...Pakuti mwamuna...

761 Tsopano, ndi ndani akuyankhula apa? Tsopano, nthawiyina dona anati, “O, Paulo anali nkhalamba yodana ndi akazi.”

762 Chabwino, tsopano pamene ife tiri apo, tiyeni tingotembenezira apa ku Agalatia 1:8, ndi kuona zomwe Paulo akunena pa izi, mwaona, mu Agalatia 1:8, inu mupeza kuti Paulo ananena apa mu Agalatia 1:8:

...ngakhale ife, kapena mngelo wochokera kumwamba, atalalikirira uthenga wina uliwonse wosiyana ndi uwu womwe inu mwaumva kale, msiyeni iye akhale wotembereredwa.

763 Tsopano musati mundide ine, mudeni Iye, mwaona.

Pakuti mwamuna ndithudi sayenera kumaphimba mutu wake, pakuti ndi mochuluka momwe iye aliri mu ulemerero ndi chifanizo cha Mulungu: koma mkazi ali mu ulemerero ndi chifanizo cha mwamuna.

764 Tsopano penyani ndime yotsatirayo:

Pakuti mwamuna si wa mkazi; koma mkazi ndi wa mwamuna.

Ngakhalenso mwamuna sanalengedwere kwa mkazi; koma mkazi analengedwera kwa mwamuna.

765 Tsopano, ine ndikutanthauza izi tsopano ndi chikondi chenicheni ndi kukoma, ndipo ine ndikuyembekeza inu mukumvetsa izo mwanjira yomweyo yomwe ine ndikunenera izi. Koma Amereka...Ngati woyenda konsekonse, Amereka ali ndi malamulo ena otsika-kwambiri, operewera a kwa akazi awo mwa fuko lirilonse mu dziko. Paris, France angakhoze kukhala nyumba ya mmwamba pambali pa momwe Amereka amawalolera akazi aawo kuti azichitira. Ndi chamanyazi!

766 Kodi inu mumazindikira kuti mulungu wa Amereka ndi mkazi? Ine ndikhoza kutsimikizira izo kwa inu ndi Baibulo ili. Ndiko kulondola. Kodi inu mukuzindikira kuti izo zimayenera kuti zibwere mwanjira imeneyo kuti mpingo wa Katolika ukhoze kubweretsamo chiphunzitso chawo cha namwali Maria?

767 Tsopano, ngati mkazi sanapangidwire kwa mwamuna, osati...Ngati mwamuna sanapangidwire kwa mkazi, koma mkazi anapangidwira kwa mwamuna, ndiye inu mungamamupembedze bwanji mkazi? Mwaona? Tsopano, nchiani chinachititsa izo, izo zinayambira mu Paris ndipo zinadzafikira mu Hollywood. Tsopano Paris amayenera kumabwera ku Hollywood kuti adzatenge azionetsero awo ndi kudzatenga mafasho awo ndi zinthu, ndi kutsikitsitsa kwa akazi athu Achimereka.

768 Ndi chiani icho kodi? Fuko lathu lafika pochepa kwambiri mpaka ngakhale atenga ntchito kuzilanda kwa mwamuna, ndi kuwaika akazi kunja kuno mu malo awa, mpaka nainte pa zana a iwo, pafupifupi, ndi aziwerewere. Ndipo mukakamba za amuna kukhala kuti apita, zedi, nchifukwa ayika akazi kunja uko mu ntchito zawo. Ndipo iwo afika potsika kwambiri mpaka akuwaika akazi ngati osungitsa bata pa msewu. Ndicho chamanyazi kwa fuko lirilonse! Inde, bwana. Kodi iwe uchita chiani nazo?

769 “Kodi inu mumachita chiani nazo, M’bale Branham?” Ine ndiyenera kuzilemekeza izo, ndine mbadwa ya Chimereka, ine ndimachita zomwe bwana wamkulu ati ndizichita. Ngati ine konse... Ngati—ngati banja litataya konse ulemu wake kwa banjalo (ana kutaya ulemu kwa kholo), banja limenelo laphwasuka mzidutswa. Ngati—ngati mpingo utaya konse ulemu wake kwa m’busa wao, bwanji mpingo umenewo wapita. Ndipo ngati fuko litaya konse kulemekeza kwawo kwa bwalo lalikulu la mulandu ndi kugamula kwake, fuko limenelo lapita mzidutswa. Ndizo ndendende kulondola. Ife tiyenera kuti tizizilemekeza zinthu zimenezo chifukwa iwo ndi abwana aakulu, mwaona. Koma si zolondola pakuyamba pomwe. Mwamtheradi!

770 Kodi inu mumadziwa kuti munthu mu Baibulo... Genesis, mutu wa 1, pamene Mulungu anamulenga mkazi n—ndi mwamuna, nampanga mwamuna ndi mkazi, ndipo Mulungu anamuza Eva kuti “mwamuna wako azilamulira pa iwe, akhala wokulamulira wako”? Yankhula izo mu Amereka ndi kuwona zomwe uti upeze! Mnyamata, si zimenezo, mkazi amalumulira pa mwamuna; iwo ayenera kumachita zimenezo, malo awamba akhazikitsidwa...

771 Ine ndikhoza kuwabweretsa akazi, ngati ine ndikanafuna kutero, kuchokera ku chipinda changa uko, mwa madzeni, akazi olemekazeka... Ine sindikunena kuti akazi onse nthawizina sayenera kuti azigwira ntchito; mwinamwake ali ndi mwamunake wodwala kapena chinachake, ndipo iwo amayenera kuti azigwira ntchito. Koma ngati iwo sakusowa kutero, iwo asamachite izo. Malo awo ndi kunyumba, kanyumba kachifumu, uko ndiko ndendende komwe iwo ayenera azikhala ali.

772 Ndipo akazi athu Achimereka akhala nawo mwayi wopita ndi kumakadya ngati nkhumba kapena afa. Ngakhale mwa zinyama zonse ndi zina zotero, pamene chinthu icho chichitika, icho chimatenga malo ndipo icho chimatsitsa khalidwe la mtundu wonsewo ndi izo.

773 Kuli mbalame yaing’ono ku Afrika, ndipo iyo ndi mbalame yeniyeni yotoleza.

774 Tsopano, mwachizolowezi, yaikazi nthawizonse imakhala yonyansitsa ya ziwiri. Yaimuna nthawizonse ndiyo yokongola kwambiri, gwape wamphongo, mbawala yamphongo, nkhanganga

yaimuna, n—nkhuku yaimuna, ndipo nthawizonse ndiyo mochuluka. . . Chifukwa, yaikazi ndi mbalame yapakhomo. Iyo imakhala pa chisa, iyo imawalela aang’ono ake. Iyo imalimbana ndi mphamba, njoka, nkhandwe, chirichonse choonjezerapo, mwaona, kuti ilere aang’ono akewo.

775 Koma mu mtundu momwe kuti. . . kapena mu gulu l—lomwe—mkazi uyo, kapena chachikazi, chimapambana pa kukongola, nthawizonse ndi mtundu wotsikisitsa. Mu Afrika, inu mukaitenga mbalame. . . Kuli mbalame yaing’ono uko, ndi imodzi yokhayo mu dziko lonselo yomwe ine ndikuidziwa, yomwe yaikazi ili yokongola kwambiri kuposa yaimuna. Ndipo pamene iyo itero. . . M—mbalame imeneyo ndi yachiwerewere mowirikiza. Iyo imayendayenda kuti ipeze yaimuna, ndi kuthamangira kunjani ndi kukaika mulu wa mazira itakomana ndi ina, ndipo imasiya yaimunayo kuti izikhalira mazirawo pamene iyo imapita ndi kukasaka yaimuna ina. Ndi ndendende kulondola. Mwaona? Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

776 Umu, tsopano taonani, mu Amereka lero, pa akazi athu. Mnyamata wochokera ku Kentucky anandiuzwa ine, masiku angapo apitawo, kuti uko kunali akazi eyiti handiredi akugwira ntchito mu fakitole yina yake kuno ku Kentucky. Ndipo iye anati, “Ine ndikhoza kumverera wotetezeka kulumbira kuti mazana anai a iwo ndi mwamtheradi achiwerewere mu msewu, ndipotu akazi okwatiwa ali ndi ana.” Mnyamata mmodzi anamutengera mkazi wake kumeneko ndi kumakamugwiritsa iye ntchito ndi gululo, ndiyeno anatsala pang’ono kuti amuphe iye. Ndipo wina ankafuna kuti amuwombere mwamuna. Ndi wina anachekana ndi kumenyana. Izo zisamakhale choncho. Uko si kukhoza.

777 Muikeni mkazi mu khitchini abwerere komwe kuli malo ake, ndiye chirichonse chikhala bwino bwino. Koma inu mukamuika iye kunjani uko ku ntchito zapagulu, iye wapita. Mwam— . . . Ine sindikunena kuti. . .

778 Akazi Achimereka amafwenthetsa mmwamba mphuno zawo ndi kumati, “Palibe kanthu kwa Izo.” Ndipo, “Inu ndisonyezeni ine.” Ndithudi, inu muyenera kumachita izo, chifukwa Baibulo linaneneratu kuti inu muzidzachita izo. Inu muyenera kumachita izo.

779 Ndipo kuno pamene. . . Izo zinali mwakuti, nthawi yaitali kalelo, mu mpingo wa Methodisti, ngati mkazi adula tsitsi lake, iye ankaikidwa kunjani kwa mpingowo. Ndithudi, iwo ankachita izo. Inde, ndithudi. Anazerini, Pilgrim Holines, Achipentekoste, onsewo anali kumachita izo. Chinachitika ndi chiani?

780 Inu mukudziwa chifukwa chake? Inu muli ndi achikazi ena kuseri kwa guwa. Ndizo ndendende kulondola. Winawake akuwopetsa chitupa chake chazakudya. . . kuwopa kuti inu muwachotsa iwo, nkuwathamangitsa iwo achoke mu mpingo.

Iwo analibe ulemu womwe woti ayime, kuima pa Mawu a Mulungu kaya Iwo upweteka kapena Iwo sutero. Ndi ndendende kulondola.

781 Mvetserani apa, mwamuna ndi wolamulira. Inu musati muziganiza kuti mukulamulira mu nyumba. Inu si wolamulira mu nyumba. Ndinu mwamtheradi... Inu si kapolo tsopano, koma ndinu wothandizira. Ndipo Adamu... Mwamuna ali ndi ulamuliro pa mkazi wake, ndipo iye ali ndi udindo pa mkazi wake yekhayo. Mulungu amamupangitsa kuti aziyankhira pa mkazi wake. Tsopano, werengani ndi kuwona ngati Mulungu akunena izo tsopano.

Pakuti mwamuna ndithudi sayenera kuti aziphimba mutu wake, pakuti mochuluka monga iye ali mu chifanizo ndi ulemerero wa Mulungu: . . .

782 Mulungu si mkazi, Mulungu ndi mwamuna. Inu mukudziwa pamene iwo amamupanga namwali Maria ndi zonse izo, ndi kupemb- . . . kapena kupembedzera ndi chirichonse monga izo, ndi kupemphera kwa namwali Maria, inu mukudziwa chomwe izo zimandikumbutsa ine? Mulungu wamkazi wamkulu Diana, yemwe Paulo anamudzudza ndi kumuthamangitsa. Ndiko kulondola. Iye anati, “Chiani, Mulungu si mkazi!”

783 Mwala unagwera uko mmunda, ndipo iwo anati mulungu wamkazi anawaponyera pansu chifano chawo, ndi chifukwa mkazi ku Korinto, ndi mpaka uko, a . . . omwe ankapembedza Diana, iwo ankafuna kuti azikhala alaliki.

784 Iwo anati, “Bwanji, mzimu unatiuza ife kuti ife tikhoza kumalalikira.”

785 Iye anati, “Chiani? Kodi Mawu a Mulungu anachokera kwa inu, ndipo kodi iwo anachokera kwa inu nokha? Ngati munthu aliyense akudziganizira yekha kuti ndi wauzimu kapena mneneri, musiyeni iye avomereze zomwe ine ndikuzinena kuti ndi malamulo a Ambuye: msiyeni mkazi azikhala chete ndi kukhala pansu mwa kumvera mu mpingo, osati kuti aziphunzitsa kapena kukhala ndi ulamuliro uliwonse.” Ndizo ndendende! Ndi zomwe Lemba linanena. Mwaona? Ndipo Mulungu adzalipangitsa gulu la alaliki kuti lidzayankhire izo pa Tsiku la Chiweruzo.

786 Chabwino, mvetserani! Inu mukuti, “Chabwino, ine ndikukuuzani inu, ine ndinaphunzitsidwa zimenezo.” Inu mukudziwa bwinoko tsopano! Ndiko kulondola. Ngati inu kapena winawake ayamba kutenga muyezo wa mankhwala, ndipo winawake nkukuuzani inu kuti ndi okupha, ndipo inu—ndipo inu nkupitirira ndi kuwamwa iwo mulimonse, ilo ndi vuto lanu lanu zotsatira apo. Mwaona?

787 Tsopano mvetserani kwa izi:

Pakuti mwamuna si wa mkazi; koma mkazi ndi wamwamuna.

Pa chifukwa ichi mkazi ayenera kuti azikhala ndi mphamvu pa mutu wake chifukwa cha angelo.

788 Aliyense wa inu akuwerenga izo? I Akorinto, mutu wa 11, ndi ndime ya 10. Ngati inu mungazindikire, “mphamvu,” (chifukwa chiani?) “za angelo,” I Akorinto, chifukwa mngelo ndi mwamuna, mtumiki. Penyani, ndi “a” wamng’ono kachiwiri. Pamene angelo akukhudzidwa, Angelo Akumwamba, ndi “A” wamkulu “A” wa chilembo chachikulu. Pamene pali “a” wamngono ndi angelo a anthu.

Ngakhale ziri choncho palibe mwamuna... kapena mkazi, ...palibe mkazi wopanda mwamuna—mwamuna, mwa Ambuye.

Pakuti monga mkazi ali wa mwamuna, chomwechonso ali mwamuna nayenso mwa mkazi;... zinthu zonse ndi za Mulungu.

Weruzani...nokha: kodi ndi kololedwa kuti mkazi azipemphera kwa Mulungu (ali ndi tsitsi lalifupi) wosadziphimba? (ganizirani za izo tsopano)

789 Tsopano penyani:

Kodi ngakhale chirengedwe chomwe sichimakuphunzitsani inu, kuti, ngati mwamuna akhala ndi tsitsi lalitali, ...

790 Mukuti, “Kodi izo zinkaimira chiani?” Tsitsi. Kodi inu simukuwona zomwe Paulo akuzikamba? Tsitsi, tsitsi lalitali! Ngati...Mkazi amayenera kuti azikhala ndi tsitsi lalitali. Ndime ya 14 tsopano:

Kodi ngakhale chirengedwe chomwe sichimakuphunzitsani inu, kuti, ngati mwamuna akhala ndi tsitsi lalitali, ndi chamanyazi kwa iye?

791 Inu mukuzimva izo? Ndi chamanyazi kuti mwamuna akhale ndi tsitsi lalitali, koma mkaz-...awo ndi malo a mkazi. Mulungu anamupanga mwamuna mosiyana ndi mkazi, ziwalo ndi mu mawonekedwe, ndi mu china chirichonse. Iye sayenera kuti azivala chovala...Baibulo linanena kuti “Ngati mkazi avala zazifupi kapena chovala chirichonse chomwe chiri choyenera kwa mwamuna, ndi themberero ndi chauve ndi nyansi pochiwona pamaso pa Mulungu.” Ndipo Mulungu adzamupangitsa iye kulipira chifukwa cha izo. Kodi inu muzimvera kwa ndani? Koma ilitu ndi Baibulo!

792 Ndipo inu mukamathamanga pozungulira kumati, “Bwanji, ine ndikuganiza ndi zabwino kwa...kumuwona akazi atavala zazifupi.” Koma Mulungu anawapanga iwo mosiyana, Iye amafuna kuti iwo azivala mosiyana.

793 Ndipo Baibulo linati, “Ngati mkazi atangoti avale konse chovala choyenera kwa mwamuna, ndi themberero.” Inu mukudziwa chomwe *themberero* liri? Ndi “chinachake chomwe chiri chauve pa kupenya kwa Mulungu.” Ndipo Yehova Wamkulu ndi yemwe amayang’ana pansu pa inu ngati chinthu chauve. . . Ndipo Baibulo linati. . .

794 Ndipo inu omwe mumati. . .Ena a inu akazi tsopano, kwa atsikana anu aang’ono amu usinkhu wa mmateni, eitini, usinkhu wa zaka twente, mumawalola iwo azithamanga kuno atavala monga momwe iye alirimo!

795 Ndipo inu, nanunso, amai! Mukuona? Pamene inu mumapita kunja ndi kumavala zazifupi izo ndi zinthu ndi kumakhala. . . ndi kumakafika ku msewu, n—ndi kukhala muli ndi tizovala ito tomwe iwo akupanga masiku ano, ndi kukupangitsani inu kuti muziwoneka ngati chinachake chomwe inu simuli. Mwaona? Ndipo inu mumapita kunja uko pa msewu mukuwoneka yense mwachigololo, inu mukhoza kukhala wosalakwa basi ndi wangwirowo pamaso pa mwamuna wanu ndi chirichonse, koma ngati inu mumapita kunja pa msewu ndipo amuna nkumayang’ana pa inu chifukwa inu munadzionetsera nokha monga choncho, ndinu wolakwa, ndipo mudzakayankha pa Tsiku la Chiweruzo chifukwa chochita chigololo ndi mwamuna aliyense yemwe akuyang’ana pa inu choteroyo. Ndi chomwe Baibulo linanena.

796 Baibulo linati, “Aliyense yemwe ayang’ana pa mkazi ndi kumusilira iye, wachita chigololo ndi iye mu mtima wake kale,” ndipo ndiwe wolakwa ndipo udza. . .

797 Inu mudzabwera ku chiweruzo nkudzati, “Ambuye, Inu mukuudziwa mtima wanga; ine sindinayambe ndachitapo chigololo, ine ndinakhala moona kwa mwamuna wanga.”

798 Koma apa padzakhala mwamuna, apa padzakhala wina, apa winanso, wina, wina, fifitini, twente, sate, forte a iwo ataima apo akuti, “Wolakwa ndi chigololo!” Chifukwa? Mwamuna wina anayang’ana pa iwe.

799 “Chabwino, ine ndinalibe kanthu kochita nazo.” Chabwino, nchifukwa chiani iwe unkadzionetsera wekha monga choncho? Pamene Mulungu anakuuza iwe kuti usamazivale izo, ndi themberero kuchita izo, ndipo iwe umapita nkumakamvetsera kwa *Ndani Amamukonda Susie*? Kapena nchiani izo. . .

800 Kodi inu munapeza chomwe chinachitika ndi mwamuna wa *Ndani Amamukonda Susie*? Inu nonse mwaziwona izo kuno posachedwapa mu pepala. Pamene ife tinali uko ku Casper, Wyoming, izo zinatuluka. Ndipo kodi dzina lake ndi ndani? Mnyamata uja yemwe. . . pa zijazi *Ife Timamkonda Susie*, kapena zomwe mu—nchiani mu dziko zijazi? A. . . O, zomwe inu nonse mumakhala kunyumba Lachitatu usiku ndi kuphonya msonkhano wa pemphero kuti muziziwonera. Ndi chiani zija

kodi tsopano? *Ife timamkonda*... Dzina lake la ujayo ndi chiani? [Mlongo ati, "*Ine ndimamkonda Lucy*"—Mkonzi.] *Ine ndimamkonda Lucy*, mwamuna wake woyenera kukhala ali... amamenya kulikonse, wagwidwa kutali uko ku Reno, Nevada, ali ndi msungwana wachikuda, anali akukhala ndi iye kwa zaka. Ndipo nzomwe inu mumakhalira kunyumba kuti muziziwona mmalo mopita, kukamvera Uthenga. Mkazi anavomereza izo. O, chifundo! Palibe chirichonse choyera kunja kwa Yesu Khristu!

⁸⁰¹ Adalitse mtima wanu, m'bale, i—ine ndikuuzani inu—amuna inu, zina za... Inu mukuti, "O, mai, tayang'anani pa upamwamba." Enieni a—akhwangwala oyipisitsa omwe ife tiri nawo, miimba, ndi mbalame zokongola. Inu simungakhoze kuiweruza mbalame ndi nthenga zake, mwaona. Kotero musingomakumbukira zimenezo. O, mai!

⁸⁰² Tsopano penyani:

Kodi ngakhale chirengedwe... (iyo ndi ndime ya 14 ija)... *sichimakuphunzitsani inu, kuti*, ndi chamanyazi kuti mwamuna akhale ndi tsitsi lalitali? (ilo mwiniwake ndi mkazi)

Koma ngati mkazi akhala ndi tsitsi lalitali, ilo ndi ulemerero kwa iye:...

⁸⁰³ Tsopano kodi iye akuyankhula za chiani? Chisoti chomwe inu anthu Achikatolika mumachivala mu tchalitchi? Ayi ndithudi! Kuphimba pang'ono pamwamba pa mutu wanu, ndi kampango? Iye akuyankhula za tsitsi lanu!

⁸⁰⁴ Tsopano! Ndipo ngati mkazi adula tsitsi lake, iye amadula ulemerero wake, ndipo iye samalolezedwa ku guwa kuti akapemphere. Mukuona, basi nzomwe akunena apa, "Kodi ndi chinthu chozolowereka kuti mkazi azipita ndi kumakapemphera ndi mutu wosaphimbidwa?" Akutero apa, akuti, "Chabwino, iye akafuna kuti adule tsitsi lake." Ndiye mumulole iye alimete mpala ndiye. "Ndipo ngati iye ati ametedwe mpala," anati, "icho nchamanyazi, ndi chamanyazi kuti mkazi achite izo." Ndiye anati, "Iye ayenera kuti aziphimbidwa." Tsopano, ine basi—ine ndikungowerenga kalata ya Paulo. Inu nonse, ziri kwa inu mukuona.

Koma ngati mkazi akhala ndi tsitsi lalitali, ilo ndi ulemerero kwa iye: pakuti tsitsi lake linapatsidwa kwa iye likhale chophimba.

⁸⁰⁵ Kodi zanenedwa kuti iye azipatsidwa chipewa? Inu anthu Akatolika kapena inu Achiprotestanti, wina yense, yemwe amapita ku tchalitchi ndipo amafuna kuti azivala chipewa, mumati, "Chabwino, ine ndikupita ku tchalitchi, ndiyenera kuti ndivale chipewa." Ayi, inu mukuyenera muzilisiya tsitsi lanu kuti lizikula. Ndiko kusiyanita kwake. Mwaona?

. . . *pakuti tsitsi lake linapatsidwa kwa iye kuti likhale chophimba.* (ndipo ndi chamanyazi kuti iye azibwera mu tchalitchi wopanda chophimba, kumapita ku guwa kukapemphera)

Koma ngati mwamuna akhala ngati—kuti ali. . . (ine sindikukhulupirira kuti ndingakhoze kuwatchula mawu amenewo, c-o-n-t-e. . .) . . . *Makani—wa makani* (inu mukudziwa chomwe wa makani ali), *ife tiribe chizolowezi choterocho, ngakhalenso* Mpingo wa Mulungu.

⁸⁰⁶ Tsopano ngati inu mukufuna kuti mutsutse pa izo, inu tsutsanani ndi Izo. Chabwino, ngati inu mukufuna kuti mukhale amakani pa izo, “O, izo sizimapangitsa kusi yana kulikonse. Tiyeni tiwasiye iwo azipitirira. Bwanji, ine ndikuganiza si kanthu. I. . . Si zomwe tsitsi liri, mulimonse, ndi chomwe mtima uli.” Izo nzoona; ngati mtima uli molondola, tsitsi likhala liri molondola (u-nhu).

⁸⁰⁷ Pitirirani nazo, ngati inu mukufuna kuti mukhale amakani, Paulo anati, “Ife tiribe chizolowezi choterocho, ngakhalenso mu Mpingo wa Mulungu. Anati, “Ngati inu mukufuna kuti mukhale wa kumbali ya Kaini, chabwino, ingopitirirani nazo.” Koma Izi ndi zomwe Paulo ankazinena.

⁸⁰⁸ O, ndipo ine sindikutanthauza kuti ndiseke, chifukwa iyo si nkhani yoseketsa. Koma ine ndikukuuzani inu abwenzi, ndi chamanyazi kuwona momwe zinthu izi zalolezedwera kuti zizichita. I. . .

⁸⁰⁹ Mvetserani! Kwa inu, alongo anga okonedwa, ine ndikufuna inu kuti muziwoneka mwakupambana kwanu ndi kukhala mwa kupambana kwanu, ndi chomwe inu muyenera kuti muzikhala muli. Ndi chomwe inu muyenera kuti muzikhala muli. Ndipo inu mukuyenera kuti muzikhala okoma ndi ofewa ndi chirichonse momwe inu mungathere pamene amuna abwera, chimodzimodzi monga momwe uyo anali wapamtima wanu. Ndipo inu mukuyenera kumakomana naye iye pakhomo ndi basi—ndi mpsyopsyono wokoma kwa iye momwe izo zinaliri tsiku lija lomwe inu munamupsyopsyona iye paguwa kuti akhale mwamuna wanu. Ndiko kulondola. Ine sindikukutsutsani inu chifukwa chowoneka mwakupambana kwanu ndi kukhala mwa kupambana kwanu. Ndipo ine ndikufuna inu kuti muzikhala mwanjira imeneyo, Mulungu akudziwa kuti ine ndikutero.

⁸¹⁰ Kuno nthawi ina pakale, ine ndinali kuyankhula kwa Jack Schiller. Ndani anayamba wamvapo za Jack Schiller? Mlaliki wotchuka kwambiri yemwe Amethodisti ali naye. Iye anati, “Mkazi anabwera nati. . . tsitsi lonse lonyansa, ndipo akutafuna chingamu, ndipo zovala zake ziri mwatheka pa iye, anati, ‘Inu mukudziwa, mwamuna wanga sakufuna kumakhala ndi ine panonso.’”

811 Iye anati, “Ine sindingamutsutse iye.”

812 Uko nkulondola, tsopano. Koma chomwe iwe ukuyenera kumachita, iwe umayenera kumakhala mu njira yoyenera. Musati muzitengera kufewa kwanu ndi kukongola kuchokera ku Hollywood, zikutengerani iko kuchokera mu Baibulo, pamaso pa Mulungu. Khalani dona, zichitani ngati dona, zivalani ngati dona, khalani awukhondo. Zichitani monga dona, musati muzivala izo. . .

813 Mwamuna aliyense yemwe amamulola mkazi wake kumapita kunja ndi kumavala tinthu tating’ono ito pamaso pa amuna, ndi tinthu tating’ono ito. . . kutuluka panja pa bwalo ndi kumatchetcha bwalolo, ndi zinthu monga choncho, bambo, ine ndikukuuzani inu, m’bale! Ine sindiri—ine sindikutanthauza kuti ndikhale woipa, i. . . Mulungu akudziwa kuti uwo ndi mtima wanga. Koma ine ndidzayenera kutero. . . Ine ndidzayenera kuti ndidzasinthe mochuluka kwambiri ndisanamulole wanga kuti azichita izo. Ine ndizikhala bwana pamwamba pa phiri apo utali wonse momwe ine ndingathere, inu mukuona; ndipo pamene ine sindingathe kutero, ine ndiyenera kuti ndisunthe nkuchokapo. Ndiko kulondola.

814 O, m’bale, ndi chamanyazi ndi chopanda chisomo kuti akazi azichita izo. Ndipo i—ine sindikutanthauza, mlongo. . . I—ine sindiri kukutsitsani inu, ine ndikungoyesera kunena kuti. . . Mpingo wathu kuno ulibe mamembala, anthu amangobwera kuno. Koma ino ndi nyumba ya Mulungu, ndipo ife mwamtheradi timawauza anthu kuti asamavale zinthu zimenezo. Kutu izo. . . inu mudzakaziyankhira izo pa Tsiku la Chiweruzo. Tsopano penyani apa. Ndipo zililolani tsitsi lanu kuti lizikula, mwaona, ndi kukhala dona.

815 Tsopano:

Tsopano mu izi ndiko kuti. . . ine ndikunenetsa kwa inu ine sindiri kukutamandani inu ayi, kuti inu mumabwera palimodzi kwa. . . osati kwa zabwinopo, koma kwa zoipirapo.

Pakuti poyamba pa zonse, pamene inu mubwera limodzi mu mpingo, ine ndikumva kuti pali kupatukana pakati panu; ndi zina zotero, . . . (izo zikupitirira tsopano ku gome la mgonero)

816 Tsopano mveterani kwa Izo. Ndi chifukwa chake kuti angelo. . .

817 Tsopano, M’bale Palmer, ine sindiri kukuuzani inu pa tepi iyi, inu zilalikirani chinthu chomwecho kumusi uko chomwe ine ndikuchita kuno. Koma inu mukudziwa bwino ndi mwabwino, ndipo inu pokhala mlaliki, inu mukudziwa kuti ichi ndi Choonadi, m’bale. Chabwino.

⁸¹⁸ Chotero *angelo* apa ndi “amuna.” Ngati inu mungazindikire izo, M’bale Palmer, izo ziri mu chilembo chaching’ono, “mngelo.” Ndipo Baibulo likupitirira . . . Iye akuyankhula za mwamuna ndi mkazi wake, mwaona, ndicho chomwe phunzirolo liri.

⁸¹⁹ Umo ndi momwe anthu amafika posokonezeka kwambiri mu Baibulo, iwo amati, “Chabwino, Mulungu akunena chinthu chimodzi *apa*, ndi china . . .” Ayi, i—inu mumachoka pa phunzirolo. Zikhalani pa phunziro lomwelo, ndizo zonse. Iye akuyankhula za mwamuna ndi mkazake.

⁸²⁰ Tsopano chinthu china chowonjezera chomwe ine ndikufuna kuti ndichigunde basi ife tisanatsekere, izo zinditengerana ine pafupi maminiti awiri:

74. Kodi oyera adzakakhala kuti ukadzatha ulamuliro wa zaka chikwi chimodzi? Ndipo kodi iwo adzakhala ali ndi matupi otani?

⁸²¹ Ine ndikuganiza ilo ndi funso lokometsetsa, ine ndikungolikonda ilo. Tsopano tiyeni tiyang’ane molunjika kumene mu ilo.

⁸²² Pa chiyambi, Mulungu . . . Ife tibwerera mmbuyo ku kuphunzitsa kwathu kwa Ahebri kwa maminiti pang’ono okha. Mulungu anali uyu, kasupe wamkulu kwambiri wa mitundu isanu ndi iwiri. Ndi angati akudziwa izo? Mukuona? Ndipo ndi angati akudziwa kuti Mulungu ali ndi mizimu isanu ndi iwiri? Mwamtheradi, Mizimu isanu ndi iwiri. Ndipo munali maso asanu ndi awiri mwa mwanawankhosa, ndi zina zotero, zonse izo zikubwera palimodzi tsopano. Mwaona? Tsopano, uyo anali Mulungu.

⁸²³ Tsopano pamene Iye (Logos) anachokera kwa Mulungu, yemwe anali Mulungu kuchokera ku kasupe wamkulu uyu kubwera mu thupi la mawonekedwe a—a munthu; ndipo izo zinapanga Logos, yomwe ife timaitcha fiofane.

⁸²⁴ Tsopano, ngati inu mutaitenga fiofane pamene inu muyang’ana pa iyo, uyo ndi munthu. Tsopano pakuti ife . . . Tsopano, umo ndi momwe ife tinali pachiyambi. Tsopano, inu simukumvetsa izo tsopano, koma inu munali kumbuyo uko pachiyambi mwanjira imeneyo. Pamene munthu anapanga . . . Pamene Mulungu anampanga munthu mu chifanizo Chake, Iye anampanga iye wa fiofane. Ndipo Iye anangomuika iye mu thupi . . . Pamene Mulungu anamupanga munthu mu chifanizo Chake, mwa mawonekedwe Ake, iwo anali . . . Mu Genesis 2, uko kunali . . . kapena Genesis 1:28, ine ndikukhulupirira izo ziri, “Uko kunalibe munthu apobe woti azilima nthaka,” ndipo Mulungu anali atamupanga kale wa mwamuna ndi wamkazi. Ndiko kulondola, “Kunalibe munthu woti azilima mu nthaka.”

⁸²⁵ Ndiye Mulungu anamubweretsa munthu chomutsitsa pang’ono mmusi ndipo anamuika iye mu moyo wachinyama, ndilo thupi ili, monga ngati zinyama chotero kuti iye azikhoza

kumalima mu nthaka, azikhoza kugwira. Fiofane ija siimagwira, iyo siimawona, kulawa, kununkhiza, kumva; zokhudzira izi zomwe ife tiri nazo. Kotero Mulungu anamuika munthu pansa apo ndi cholinga cho—choti azikhudza ndi kumverera.

⁸²⁶ N—ndipo pamene iye ankayenda kudutsa mu Munda wa Edeni, poyamba ngati fiofane, (monga Mzimu Woyera womwe uli muno tsopano ukuyenda mkati muno), iwo unkatsofolera moyo wazinyama. Iwo unkalumulira chirichonse, koma iwo sunkakhoza kumalima mu nthaka, mwaona. Chotero Mulungu anamuika iye mu mnofu chotero kuti iye azikhoza kumalima mu nthaka. Anamupatsa iye zokhudzira zake zisanu, kuti azilima nthaka ndi kukonza—minda ya mpesa n—ndi zina zotero, ndiyeno munthu ankawonekabe wosunguluma. O, ichi ndi chithunzi chokongola.

⁸²⁷ Penyani, pakuti pamene iye anapangidwa koyamba, iye anapangidwa anthu awiri palimodzi. Iye anapangidwa zonse mwamuna ndi mkazi, mwamunayo anali. Baibulo linati iye anali. Mulungu anamupanga munthu zonse mwamuna ndi mkazi, “Iye anamulenga iyeyo.” Zindikirani tsopano, pamene munthu analekanitsidwa kuchokera ku fiofane ndi kuikidwa iye mu mnofu, iye anali—iye sanali basi zonse palimodzi apo; gawo la umunthu wake linali likadali fiofane, chotero izo sizinkawoneka bwino.

⁸²⁸ Apo pankapita yamphongo ndi yaikazi mu ng’ombe, apo pankapita kavalo, ndipo apo pankapita ng’ombe, ndipo apo pankapita china chirichonse, ziwiriziwiri. Koma Adamu, iye . . . izo zinali . . . Mwaona, apo panali chinachake chikuperewera. Kulakalaka komweko kunkasonyeza kuti panali chinzake chikumuyembekezera iye. Inu mukumvetsa izo? Ndipo malingaliro omwe oti ife timayenera kufa kuno, kuti ife timavutitsidwa ndi kudodometsedwa, ndipo ife timakhumba Moyu umene ulibe imfa, izo zimasonyeza kuti iwo ukutiyembekezera ife. Mwaona?

⁸²⁹ Ndipo Adamu anali wosunguluma. Ndipo Mulungu, kuti asonyeze kuti iwo sakanakhoza kulekanitsidwa . . . Tsopano ine ndibwerera mu chinthu chomwechi, mphindi yokha.

⁸³⁰ Onani, Iye sanapite konse nakatenga dongo nkumupanga Eva, koma Iye anamupanga kuchokera ku dothi lapachiyambilo, Adamu. Iye anatenga nthiti kuchokera ku mbali yake ndipo anamupangira iye womuthandizira, ndipo ameneyo anali Eva. Iye anapangidwira kwa mwamuna, ndi gawo la mwamuna. Iye anali gawo la iye pachiyambi, mu chilengedwe, mu fiofane. Iye anali gawo la iye pansipa kuno mu chirengedwe ichi. Iye sakanakhoza kugawanizidwira mu chirengedwe china, iye ankayenera kuti apangidwe mwa chirengedwe chomwecho.

⁸³¹ Ndizo ndendende chifukwa chomwe Khristu ndi Mulungu ankayenera kukhala ali Munthu yemweyemweyo, izo

sizikanakhoza kukhala chirichonse chosiyana. Ngati iye akanakhala munthu wabwino kapena mneneri, Iye sakanakhala Muomboli; Iye ankayenera kukhala ali Mlengi Mwiniwake. Koma Iye akadali fiofane pano, inu mukuona, ndi momwe Iye analiri apo.

⁸³² Tsopano munthu anabwera pansi kuno ndipo i—iye anali wodabwitsa; ndipo Mulungu anazikhala izo, Iye anati, “Izo ndi zokongola, asiyeni iwo azikhala pa dziko lapansi ndi kumakhala apo kwanthawizonse. Ndizo zonse; k—kwa Umuyaya, mopitirira pitirira pitirira. Kulola izo zizingokula, ndipo mbewu iliyonse izibalapo, ndi chirichonse monga choncho. Ndipo lolani munthu azikhala moyo, ndi zirombo zizikhala moyo, ndi china chirichonse, kwanthawi za nthawi. Izo zonse nzabwino.” Mwaona?

⁸³³ Ndiyeno tchimo linadzalowa. Ndipo ine ndikufuna kuti ndipange neno ili. Mu . . . Anthu ochuluka kwambiri amapanga kulakwitsa kowopsya koteroko pa Lemba limodzi ili, ndipo apo ndi pa Salmo la 23. Iwo amaliwerenga Ilo monga chonchi, “Eya, ngakhale ine ndiyenda kupyola mu chigwa cha mdima wa mthunzi wa imfa.” Tsopano, palibe chinthu choterocho. Baibulo silimanena, kuti, “Mthunzi wa mdima wa chigwa . . . chigwa cha mdima wa mthunzi wa imfa.”

⁸³⁴ Limati, “Ngakhale ine ndiyenda kudutsa mu chigwa cha mthunzi wa imfa.” Tsopano, iwo usanakhale mthunzi, iwo umayenera kumakhala nako kuwala kuti kuupange mthunziwo. Mwaona, Davide pokhala mneneri ndipo ali pansi pa kudzoza, iye sanalakwitse, iye anangonena Choonadi: “Eya, ngakhale ine . . .” osati, kuyenda kudutsa mu chigwa *chamdima*, koma, “kudutsa mu chigwa cha mthunzi ya imfa.”

⁸³⁵ Ndiye inu mumayenera kukhala ndi gawo lina la kuwala kuti mupange mthunzi. Ndipo umo ndi momwe izo ziriri apa. Ife tiri zonse achibadwa ndi auzimu. Thupi ili ndi loti lidzafa, ndipo ilo linabalidwa ndi mkazi; osati ndi china chirichonse koma kupyolera . . . Osati ndi Mulungu, ndinu chopezekaponso kuchokera kwa Adamu ndi Eva. Ungakhale wakuda, woyera, kapena chirichonse chomwe iwe uli, inu ndi chopangidwapo, mphukira yochokera kwa Adamu ndi Eva. Izo zimalipangitsa thupi lanu “lobadwa mu tchimo, kuumbidwa mu kusaweruzika, kubwera ku dziko kumayankhula bodza.” Inu ndi atsoka ndi oweruzidwa pa kuyamba kwa moyo wanu, osati wopanda ngakhale mwayi.

⁸³⁶ Tsopano, chifukwa mzimu umene inu muli nawo umabwera kwa inu mwa chibadwa, ndipo mwa chibadwa kubwera kuchokera ku kugonana, kukhumbirana kwa mwamuna ndi mkazi kumabala mwana wapadziko lapansi. Ndipo mukamusiya mwana ameneyo mwayekha, ndi kusamuphunzitsa iye cholondola chirichonse, iye akula molakwika. Osamuphunzitsa

iyе ngakhale chabwino ndi choipa, iye amatenga choipa. Chifukwa ndi chibadwa chake kuti azichita zoterozo.

⁸³⁷ Mupenyeni mwana wamng'ono, wosafika pa utali chonchi, amangochita misala choncho; iye basi...i—iye amapotoza manja ake, ndi kufiira pa nkhope yake, ndi kukoka mpweya wake. Zedi. Ndi chiani icho? Ndi chibadwa chake. Iye anatengera izo kuchokera kwa abambo ake kapena amayi ake, wina; iye anali ndi kupsya mtima kokwanira kumenyana ndi macheka, kapena abambo ake. Ngati iwo sanali, agogo ake aamuna kapena aakazi anali. Mwaona, ndi mphukira.

⁸³⁸ Chotero izo zimapangitsa...Inu munabadwa mu dziko. Inu munabwera mwa chibadwa, ndipo chonse chomwe uli ndi wakuda ndi wamwaye, ndi watsoka, ndi wotembereredwa ndi wopita ku gehena. Ndiko kulondola!

⁸³⁹ Koma pamene inu mubadwa kachiwiri, ndiye Kuwala kwa Mulungu kumawalira kupita mu solo imeneyo (alaluya) ndiye sichimakhanso chigwa cha mdima, koma ndi chigwa chiri ndi mthunzi mkati mwake. Inu mukhoza kukhala muli wophimbidwa kuno ndi mnofu, ndi zinthu pa nkhope yathu, koma muli Kuwala kokwanira mmenemo. Ndipo tsiku lina Kuwala uko ndi mdima zidzayenera kuti zidzalekane! Ndipo pamene kuwala kuwala, mdima umathawa. Ndipo pamene ife tidzapita kukakhala ndi Khristu mu thupi limenelo, mdima ndi imfa zidzathawa, ndipo ife tidzatulukira mu Kuwala kwangwiro. Ulemerero kwa Mulungu! Ndi ife apo; sikudzakhalanso matenda, sikudzakhalanso mdima zitasakanizika nazo.

⁸⁴⁰ Pakali pano ife tiri nazo zonse matenda ndi chisangalalo, ndipo tirinso ndi thanzi ndi nyonga, ndipo ife tiri nazo zamkati ndi zakunja, ndi zokwera ndi zotsika, ndi chimwemwe ndi chisoni, zina zotero. Chabwino, ndi mthunzi chabe. Ife tiri nako kuwala kokwanira koti tizikhoza kudziwa kuti pali Kuwala pamenepo; ndipo ife tikadali mu thupi, mu mnofu. Koma tsiku lina Tsikulo lidzafalikira. Ndi pamene mngelo wa imfa ati adzaima pa phazi la kama, ndi pamene adotolo akuti zonse zatha; ndipo chachibadwa ichi chimabwera kuchokera ku chazimu, ndipo kuwala kumabwereranso ku Kuwala, ndipo mdima umabwerera ku mdima. Ndiye chakufa ichi chimavala chosafa. Ndi pamene chivundi ichi chimavala chisavundi, ndi pamene chakufa ichi chimavala chosafa, ndipo ife timakhalani kuchokera ku cholengedwa cha nthawi nkukhala cholengedwa Chaumuyaya. Inu simungakhoze kupita kunja uko ndi mdima wathunthu, inu muyenera kukhala ndi kuwala mu mdima. Ndi inu apo. Ndilo thupi ilo lomwe inu mumalandira.

⁸⁴¹ Kodi ife timachita chiani? Chabwino, m'bale wanga woyera wokonedwa, mlongo wanga woyera wokonedwa, asanaikidwe maziko a dziko, pamene Mulungu anakulengani inu mu

chifanizo Chake, kapena anamulenga—mwamuna mu chifanizo Chake, ndipo anamulenga mkazi mu chifanizo cha mwamuna kwa ulemerero wa mwamuna, Iye anakupangani inu wa fiofane. Monga momwe Iyemwini, pamene Iye anati, “tiyeni ife” kwa zolengedwa zomwe Iye anali atazipanga, “tiyeni ife timupange munthu mwa maonekedwe athu omwe, monga mwa kufanana nafe, fiofane.” Mulungu anali asanakhale thupi apobe, Iye anali mu fiofane.

⁸⁴² Ndipo Mose anamuwona Iye. Mose analirira, “Ambuye, ndiroleni ine ndikuwoneni Inu.”

⁸⁴³ Iye anati, “Pita uko ndi kukabisala mu thanthwe, mu mphanga.” Ndipo Mose anakalowa mu mphanga umo; ndipo pamene Mulungu anadutsa apo, mphenzi ndi bingu. . . Ndipo pamene Mulungu ankadutsa apo, Iye anali ataulozetsa nsana Wake monga *chonchi*.

Ndipo Mose anati, “Two unali nsana wa Mwamuna.” Aleluya!

⁸⁴⁴ Anali ndani Uye? Melkizedeki yemwe anabwera pansi, Mfumu ya Salemu, wopanda bambo ndi mayi, wopanda chiyambi cha masiku kapena kutha kwa moyo. Ndi Iyeyo! Ndipo Iye anabwera pansi. Ndi Iyeyo yemwe anayankhula kwa Abrahamu; anamusonkhanitsira Iye thupi laling’ono la mnofu monga choncho, ndipo [M’bale Branham akupemerera—Mkonzi.] anapumira mwa ilo, analowa mu ilo, ndipo anabwera pansi nadzadya ng’ombe yaing’ono, anamwa mkaka wochokera mu ng’ombe, ndi kudiyapo batala wina ndi zigumu zina. Ndi Angelo awiri.

⁸⁴⁵ Ndipo pamene iwo anayenda apo napita kumene kuja, ndi zinthu zonse izo nkungoti [M’bale Branham akupemerera—Mkonzi.] anasowa napita kwina.

⁸⁴⁶ Ine ndinali ndisaganizepo za izo. Kuno nthawiyina pakale, ndikulongeza chipolopolo cha mfuti, ine ndinali ndi mfuti ya .22, ndi ya Liwiro .220. Ndipo inu abale a mfuti muno mukuzidziwa. Chipolopolo chaching’ono, ndi chipolopolo cha machaka forte-eyiti, ya utali *chonchi* basi, ya chipolopolo wamba cha .22, Chimaikidwa mu thumba la mphamvu ya .30-06. Tsopano i. . . Fakitare imangolongoza izo kuti izifika mapazi forte-foro sauzande pa mphindi. Chabwino, koma inu mukhoza kuikamo wokwanira. . . kuilongoza iyo nokha, ndipo inu mukhoza kuyikamo iyo poti izifika mapazi faivi sauzande pa mphindi. N—ndipo mwa njira ina, ngati inu munali kuwombera. . . Ife tinali kuwombela, tsiku lina, pa mayadi mazana awiri, ndipo chipolopolo chinkagunda fumbi, ilo linkauluka mfutiyo isanalire konse. Ndi momwe inaliri ya liwiro.

⁸⁴⁷ Ndiye inu mukatenge chotokosera mmano (inu mukudziwa, mbali yamphwamphwa pa chotokosera mmano) ndi kufikira

mu wonga wanu ndi kudzadzitsa chinthu chanucho ndi wonga, pafupi njere zinai kapena zisanu zazing'ono zokha, ndi kuchiika icho pamwamba apo, ndiyeno nkuika chipolopolo chanu mmenemo. Nkuima apa, ndipo inu nkukhala ndi chipolopolo mdzanja lanu kwa mphindi. Ndi kuchiwombera icho kunja uko pa njira yomwe yaima mapazi thuu handiredi kuchokera kwa inu, ndipo nkumbwayo isanasunthe nkomwe. Chipolopolocho chimabwereranso ku chikhalidwe chake chapachiyambi, kubwerera ku mipweya. Pano pali chipolopolo chomwe chiri kopala ndi mikala zitasakanizikana palimodzi, ndipo mu kanusu kamodzi ka mphindi, icho chabwerera mpaka inu simukhoza kuzipezanso izo kachiwiri. Icho chabwerera mmbuyo momwe monga momwe chinaliri zaka handiredi bilioni zapitazo, kubwerera ku mipweya. Mipweya imeneyo iyenera kuti ipangike ndi kubwerera kukhala kopala ndi kukhala mkala, ndi zina zotero, monga choncho. Mipweya imeneyo iyenera kuti ikhazikike.

848 Tsopano, ndi inu apo. Ndi momwe ife tiriri kuno, ife tinachokera ku chokhalapo chapamwamba. Pachiyambi ife tinali mu mawonekedwe a Mulungu. Chophimba ndi mdima zimatitchinga ife kuti tisamazidziwe izo tsopano. Koma Yesu anawauza ophunzira ake kuti Iye “anali ndi iwo asanaikidwe maziko a dziko.” Mwaona? Ife tinali! Inu simungakhoze kuzidziwa izo pano, koma inu munali pachiyambipo. “Ndipo ngati msasa wa pansi pano uwu udzasungunuka, ife tiri nawo kale wina ukutiyembekezera!” Aleluya! Ndiyeno ife timasunthira mu fiofane iyi, chomwe ife tinali poyamba, chotero kuti ife tizikhoza kudyu ndi kugwirana chanza. Ndipo miyoyo ya pansi pa guwa ikufuulira, “Mpaka liti, Ambuye?”

849 Pali masitepe seveni amene amapita kwa Mulungu, a Mizimu isanu ndi iwiri p—pamene zikupita mmusi. Chabwino, pamene inu mupita pansi pa guwa la Mulungu, iwo anali akulira, “Ambuye, mpaka liti? Kodi ife tingakhoze kubwerera, podzera pansi apa?”

850 Mulungu anati, “Kwa kanthawi ka pang'ono kokha, mpaka anthu amzanu avutike chinthu chomwecho chimene inu munavutika nacho.” Mwaona?

851 Ndiyeno miyoyo idzabwerera kuno, ndipo iwo adzakhala amuna ndi akazi kachiwiri, ndi kukhala moyo kwanthawizonse pamene mdima wonse ndi imfa ndi matenda ndi chisoni cha mdima zazimirira; palibenso mthunzi winanso, ndi mwamtheradi kuwala kwa dzuwa!

852 Mvetserani. Ndi izi zomwe ziri. Siyani izo zikhale mwamdima momwe izo zikufunira kutero; sikungakhoze kukhala kwamdima mochuluka kwambiri mpaka dzuwa lidzaswa pang'ono paliponse pa mdimawo. Mdima ndi kuwala sizingakhoze kukhala motalika palimodzi. Pakuti...

Champhamvu kwambiri ndi chiani? Ndi kuwala. Ndipo pamene kuwala kuwala, mdima umathawa. Amen. Kodi sindinu okondwa? Kodi inu simukusangalala kuti inu mukudziwa? Mopanda kukaika, palibe mthunzi paliponse. Koma Kuwala kodala uku komwe kuli mmitima yathu pakali pano, chinachake chikuchitira umboni moyankhira: Mwana wa Mulungu, mphamvu ya Mulungu.

⁸⁵³ Ndipo ife timayenda kuno, kumapenya mphamvu ya Mzimu Woyera ikubwera pansu ndi kumapita uko mu msonkhano, ndi kumati, “Inu munali Akazi a *Akuti-n-akuti*, kuti inu munachita chinthu *chinachake*, ku malo *enaake*. Inu mwakanthidwa mliri ndi ichi motalika chotere, koma NDIZO PAKUTI ATERO AMBUYE, ‘Imani pa mapazi anu, inu mwachiritsidwa.’” Ndipo olumala ndi akhungu amaima pa mapazi awo. Ndipo mthunzi wa munthu, wodyedwa ndi khansara, nkuwuka ku moyo ndi thanzi latsopano kachiwiri.

⁸⁵⁴ Palibe zokaika, Yesu anati, “Zinthu izi zomwe Ine ndikuzichita, muzidzazichita inunso.” Ndipo Iye anati, “Ine sindimachita kanthu mpaka Atate atandiwonetsa Ine.”

⁸⁵⁵ Kodi ndi chiani izo? Uko ndi Kuwala komwe kwabwera nkudzasakanizikana mu mdima uwu, inu mukuona, kuti kutiwombole ife. Mukumva zomwe ine ndikutanthauza?

⁸⁵⁶ Tsopano, tsiku lina zidzabwerera uko komwe, ndiyeno pamene fiofane idzakhala mnofu wosafa kachiwiri monga izo zinali pachiyambi, ndiye Yesu abwera, ndipo Mulungu... pamene Khristu adzakhala ali mmodzi. Khristu adzakhala pa Mpandowachifumu, ndipo anthu onse adzakhala ali aumunthu. Khristu adzakhala ali pa mpandowachifumu wa Davide, munthu, Ambuye Yesu; osadzafanso. Ife sitidzafanso, ife sitidzakhalanso odwala, sitidzakhalanso ndi chisoni, ndipo ife tidzakhala moyo kupyola mu zaka chikwi.

⁸⁵⁷ Ndipo pamene zaka chikwi zidzatha pa dziko lapansi lino, ndiye Mdierekezi akutulukira apo; ndipo chiukitsiro chachiwiri chidzabwera, chiukitsiro cha osalungama. Iwo adzasonkhanitsa ankondo awo ochuluka monga mchenga wa ku nyanja, ndipo iwo adzabwera apo kudzauzinga msasa wa oyera, ndipo pamene iwo adzatero, Mulungu adzavumbitsa moto ndi miyala ya sulfure kuchokera kumwamba ndi kuwaononga iwo.

⁸⁵⁸ Ndipo Yohane anati, “Ine ndinawona kumwamba kwatsopano ndi dziko latsopano, pakuti kumwamba koyamba ndi dziko loyamba zinali zitapita, ndipo uko kunalibenso nyanja. Ndipo ine, Yohane, ndinawona Mzinda Woyera, Yerusalemu Watsopano, ukutsika kuchokera kwa Mulungu kuchokera Kumwamba, wokonedwa monga mkwatibwi atakometsedwera kwa mwamuna wake.” Ndi inu apo.

⁸⁵⁹ Apo iye anati, “Mkazi...Mwanawankhosa ndi Mkwatibwi adzakhala umo kwanthawizonse.” Ilo lidzakhala

dziko latsopano, mamilioni ndi mamilioni a mailosi a mphwamphwa. O, mai. Mzindawo, Baibulo likuyeza Mzinda wamphwamphwawo mailosi fifitini sauzande konsekonse, ndi mailosi fifitini sauzande mlitali, fifitini sauzande mailosi kutambalala, ndi fifitini sauzande mailosi mmwamba. Ndizo ndendende kufotokoza komwe Baibulo limapereka kwa Mzindawo. Palibe zodabwitsa kuti uko kulibenso nyanja, apo panalibe malo a iyo.

⁸⁶⁰ O, kudzakhala kuli kukongola koteroko! Ndipo mkati umo, muli kasupe cha ku Mpandowachifumu wa Mulungu komweko, umene umayendera ku Mpandowachifumuwo. Kuli mtengo ku mbali iliyonse ya mtengo...ya mtsinje wa Moyo. Ndipo mu mtengo uwu muli zipatso za mitundu thwelofu, ndipo iwo umapereka chipatso mwezi uliwonse.

⁸⁶¹ Uko kuli akuluakulu twente foro. Uko kuli Mkwatibwi. Uko kuli forte ndi foro sauzande, adindo amkachisi. O m'bale, ife tikupita kwinawake! Zinthu zomwe ziri patsogolo kwa ife. Foro...Akuluakulu twente ndi foro. Adindo handiredi n forte-foro sauzande. Mkwatibwi ali ndi Khristu. Mai, inu mukayankhula...Kwathu, Kwathu kokoma! Amen.

⁸⁶² Kuganiza kuti ine ndiri nawo mwayi wopita uko, ndipo inu muli nawo mwayi wopita kumeneko. Ndipo inu mungasankhirenji inu kuti muziyenda mu mdima uwu ndi kusamawona Kuwala kulikonse, ndi kufa nkupita mu chisokonezeko ndi kusakhala kanthu? Pakuti pamene Kuwala kutenga ulamuliro wake wapamwamba, sipakhalanso malo a mdima. Pitani kafufuzeni kumene mdima unapita pamene kuwala kunadza. Ndi momwe izo ziriri, pamene zinthu zonse zitembenezidwira kwa Mulungu. Izo zinali...mdima unali ndi chiyambi, mdima uli nawo mapeto. Kuwala kunalibe konse chiyambi kapena sikudzakhala konse ndi mapeto. Mulungu analibe konse chiyambi kapena alibe konse mapeto. Chotero, tsiku lina, dziko lonse losokonezekali ndi tchimo lake lonse ndi kukongola kwake, kotchedwa chomwecho, ndi zosangalatsa zake zonse ndi zomverera, ndi zapamwamba zake zonse ndi chirichonse zidzazimirira nkusakhalanso kanthu, ndipo izo sizidzakhalaaponso. Izo sizidzakhalaaponso, sipadzakhalanso kuganiziridwa kwake! Ilo linati, ngakhale, "Izo sizimadzafika pokumbukiridwa kenanso."

⁸⁶³ Koma odala a Ambuye nthawizonse azidzakhala ndi Iye. Ife tidzakhala nalo thupi longa thupi Lake lomwe laulemerero; ndipo tizidzakhala ndi Iye, ndi kumadya ndi Iye, ndi kukhala pansu ndi Iye, ndi kukhala limodzi ndi Iye kwanthawi ndi kwa nthawi ndi kwa nthawi zosawerengeka; ndipo mibadwo Yamuyaya izidzapitirira mu dziko lopanda mapeto.

⁸⁶⁴ Ndipo inu muli nako kusankha usikuuno. Ngati inu simunakonzeke kuti mukakomane ndi malo amenewo, ziribe

kanthu momwe inu mumapitirira ku mpingo, kaya ndinu membala wabwino chotani, inu mwataika mpaka Khristu atakupatsani inu Moyo watsopano mu mdima uwo womwe inu mukuyendamo. Inu mukhoza kukhala wachipembedzo. Wachipembedzo... Tamvera, mzanga, chipembedzo ndi chaluntha. Mukuona? Ana onse a Kaini nthawizonse anali nacho chipembedzo. Ayuda aja anali nacho chipembedzo pamene Yesu anabwera, koma iwo anakana chipulumutso.

⁸⁶⁵ Inu mukhoza kukhala achipembedzo kwambiri usikuuno. Inu mukhoza kukhala Achipresbateria, Achimethodisti, Achipentekoste, Achinazereni, Achipilgrim Holiness. Inu mukhoza kukhala achipembedzo basi; kumapita ku mpingo wanu ndi kumakachitira umboni, inu mukhoza kumaimba ndi kumafuula ndi kumamutamanda Ambuye, inu mukhoza kumabweretsa chakhumi chanu ku mpingo, inu mukhoza kumawachitira oyandikana nanu mwabwino, izo ziribe kanthu kamodzi kochita ndi kopita kwanu Kwamuyaya. Kaini anachita pang'ono paliponse pa izo. Mwamtheradi.

⁸⁶⁶ Baibulo linanena kuti “tirigu ndi nansongole zidzabwera palimodzi.” Tirigu wamng'ono wakaleyo atakhala, akuchitira ludzu mvula, ndi—minga nazonso. Pamene mvula ibwera, minga imangokhala yosangalala basi kuti ipeze mvula monga tirigu aliri. “Koma, ndi zipatso zawo, inu mudzawadziwa iwo.”

Tsopano tiyeni ife tipemphere pamene inu mukupima zipatso zanu:

⁸⁶⁷ Tsopano, Atate, Mulungu, pakhala pali mafunso okhwima pano usikuuno. Ine mwina sindinachite chinthu choyenera, koma mwakukhoza kwa kudziwa kwanga; Inu mukuudziwa mtima wanga. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu muzilandire izo. Ndipo tsopano, mwinamwake, mu mafunso ena awa, ngati ine sindinazipange izo molondola, ndiye Inu muyankhule kwa mitima ya anthuwo, ndipo Inu muwapange iwo basi chomwe iwo akuyenerera kukhala ali. Ine ndikumverera kuti Inu munandiuza ine. Koma ngati ine ndingakhale ndi kulakwitsa, ndiye Inu mundikhululukire ine.

⁸⁶⁸ Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, kuti aliyense wa awa azitengere zinthu izi mu mtima mwawo, ndipo mulole iwo alingalire pa izo ndi kuganiza monga chonchi, “Inde, pali mpingo, pali zinthu izi. Ndi zomwe Baibulo linanena.”

⁸⁶⁹ Mwinamwake madona, Ambuye, Inu mukudziwa ine sindimatanthauza kalikonse konena wina kupatula kuwauza iwo. Koma, Mulungu, i—ine ndimawakonda alongo anga, ndipo Inu mukudziwa zimenezo, Atate. Inu mukudziwa momwe ine ndimalingalirira za iwo. Koma kuti ndiime ndi kumawauza iwo chinachake cholakwika, ine ndingakhale—wachinyengo kwa iwo. Ine sindikufuna kuti ndikhale wachinyengo kwa alongo

anga, ine ndikufuna kuti ndiziwauza iwo Choonadi. Ndipo, Atate, ine ndazitenga Izo kuchokera mu Mawu Anu omwe.

⁸⁷⁰ Ndipo tsopano ine sindikuwaweruza abale anga, koma, Ambuye, ine ndikunena kuti iwo akhala akulakwitsa pamene iwo akhala akuloleza zinthu izi. Ndipo ngati dona amadziwa mosiyana napita namakachita izo, ndiye ziri ndi iye, m'busa alibe mulandu.

⁸⁷¹ Abba Atate, zinthu izo ndi Mawu Anu, ndipo izo ziri kwa Inuno. Tsopano Inu yankhulani kwa mitima ya anthuwo. Ine ndikuwapereka iwo onse kwa Inu. Ine ndiwona zomwe Inu mwachita, Atate; Inu mukudziwa. Yankhulani kwa mtima uliwonse. Ife tikupempha mu Dzina la Khristu.

Ndi mitu yathu yoweramitsidwa:

⁸⁷² Ine ndikudabwa ngati winawake angakweze dzanja lake, nkuti, “M'bale Branham, ingondikumbukirani ine kuti ine ndikhoze kukhala mgonjetsi kwathunthu, ndipo pa tsiku lotsiriza ndidzavale chovala cha chikwati ndi kudzakhala ndi Khristu.” Kodi inu mungakweze dzanja lanu, nkuti, “Ndipemphererene ine”?

⁸⁷³ Aliyense akhale mutu wake uli panso tsopano, ndi kungowerama. Mulungu akudalitseni inu, ndizo zabwino. Apo, Mulungu akudalitseni inu, alongo anga; ndi abale anga, nanunso, mukukweza manja anu. Ndizo zodabwitsa.

⁸⁷⁴ Tsopano, Atate, Inu mukuwaona manja awo. (Ine ndikudziwa, nthawizina iwe umaganiza, “Chabwino, kapemphero kakang'ono kokha monga ako?”) Mulungu, ine ndikuganiza za amayi aja, anati dzulo, “Kapemphero kakang'ono kokha uko mu nyumba yake tsiku lijali pamene mnyamata uja anali kufa, masabata atatu kuti akhale moyo, chotupa chiya pa ubongo, ndipo tsopano izo zinasintha zinthu.”

⁸⁷⁵ Ine ndikuganiza za Hezekia, atatsamiritsa nkhope yake cha ku khoma, ndipo akulira, “Ambuye, ine ndikukupemphani Inu, kuti mundichitire ine chifundo. Ndilingalireni ine, pakuti ine ndayenda pamaso Panu ndi mtima wangwiwo.” Izo zinasinthitsa kuchokera ku imfa kupita ku moyo.

⁸⁷⁶ Kufuula kumodzi kochokera kwa Mwana wa Mulungu, “Lazaro, tulukamo!” ndipo munthu wakufa anabwerapo.

⁸⁷⁷ O Mulungu, Inu munati, “Yankhulani, pemphani, ndipo zidzapatsidwa. Pamene inu munena chirichonse, khulupirirani kuti zomwe inu mwanena zifika pochitika, inu mudzakhala nazo zomwe inu mwanenazo.”

⁸⁷⁸ Tsopano, Atate, ine ndikupemphera kuti aliyense yemwe anakweza dzanja lake alandire zomwe iwo anakwezera manja awo. Mulole iwo kuti adalitsidwe. Ndipo Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu muwathandize alongo athu, kuti iwo akhale. . . muwalole iwo azidzikhaliitsa ndi khalidwe, kuti

Satana kupyolera mu televizioni ndi magazini a *Nkhani Zoon* ndi zina zotero, zomwe zagwiritsidwa ntchito mosasamala, ndi maprogramu osadulamo zoipa, momwe nyansi ndi zolaula za pa televizioni ndi zina zotero, zomwe zikanati. . . Yomwe ikanakhala chida chopindulira miyoyo mamilioni kwa Inu, koma momwe ziriri zosadulamo zoipa, ndi kuchotsamo zinthu zonse zonyansa izi zomwe iwo. . . O, ndi zachisoni bwanji! Ndipo podziwa kuti mzimu wa Mdierekezi walowa mmenemo ndi kuwazungulira alongo athu, ndi kuyesera kuti awapange iwo kukhala ndi kumavala monga choncho.

⁸⁷⁹ Ndipo ife tikupeza kuti m. . . mwa abale athu, nawonso, Ambuye, kuti momwe iwo amalingalira kuti iwo akhoza kumasuta ndi kumamwa, ndi kumapitirira nazo monga choncho, ndi kukhalabe ali Akhristu chifukwa iwo amati “amakhulupirira.” Aloleni iwo adziwe kuti “Mdierekezi amakhulupirira, nayenso.” Ndipo iye si wopulumutsidwa, “iye amakhulupirira ndipo amanjenjemera.”

⁸⁸⁰ Ndipo tsopano, Atate, ife tikupemphera kuti Inu mukhale achifundo kwa ife tonse, ndi kutikhululukira ife za machimo athu, ndipo mwina ena sanakweze manja awo, O Mulungu, khalani achifundo. Mulole mwayi wotsatira womwe iwo ati akhale nawo, mulole iwo akweze manja awo.

⁸⁸¹ Ife tikukonzekera kuti titenge mgonero, Ambuye. Tikhululukireni ife pa zolakwitsa zathu ndi moyo wathu wammbuyowo. Ndipo mulole kuti ife tilandire za mdalitso Wanu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Khristu. Amen.

⁸⁸² Ambuye akudalitseni inu. Ine ndikupepesa kuti ndakusungani inu monga chonchi. Ine ndimangodabwa, basi mgonero usanachitike, ngati pali aliyense ati abwere kuti adzapemphereredwe, akufuna kuti apemphereredwe, chabwino, ife tikhala okondwa kuchita izo pa nthawi ino basi, ngati alipo aliyense woti apemphereredwe.

⁸⁸³ Chabwino, m'bale, inu mubweretseni iye pamwamba pomwepa, izo zikhala bwino. Ndipo mphindi yokha, ndiyeno ife t—ife tibalalitsidwa. Ndiyeno pamene ife tabalalitsidwa, ndiye iwo omwe akufuna kuti atsalire ku mgonero, akhoza kutsala. Koma pakali pano tikuti tiwapempherere odwala. Kodi Baibulo linati chiani?

⁸⁸⁴ Ngati m'baleyo sangawukepo. . . Ziri bwino, ingomusiyani iye akhale pamenepo, ife tibwera kwa iye. Izo ziri bwino, ingomulolani iye kuti akhale pomwepo. Ndipo ife tibwera apo pomwe ndi kudzamupempherera iye. Ziribwino. Chabwino, bwana, basi—ingomulolani iye kuti akhale pomwepo. Ndi zovuta kuti iye aime pano, bwanji, ife tikhala okondwa kubwera kwa iye komweko.

⁸⁸⁵ Tsopano ine ndikufuna kuti nditchule chimodzi chaching'ono ichi, mzanga wokondedwa. Ukuona, i—ine

ndikudziwa kuti Ambuye atsimikizira izi mobwereza bwereza nthawi zochulukira kwambiri. Mwaona? Ine si mlaliki mochulukira, ine ndiribe maphunziro ndi zina zotero. Ine ndimawakonda Ambuye Yesu, Mulungu akudziwa kuti ine ndimamukonda Iye. Koma chinthu chimodzi chomwe ine ndinaitanidwira kuti ndizichita, nkupempherera odwala. Inu mukukhulupirira izo? Ngakhale ine ndisanadziwe konse za mphatsoyo, ine ndinkakonda kupita uko ku chipatala; ndipo ine ndikukumbukira anamwino aja akuti, “Tsopano inu mukhala bwino.” Mwaona? Ndi basi chinachake, chomwe Mulungu wakhala wachifundo kwambiri pa kulemekeza mapemphero anga a kwa anthu.

⁸⁸⁶ Ine ndikulingalira, usikuuno, ngati akanati awaitane, basi kulengeza kwa ku dziko lonse kulikonse mu dziko. Ndi kuti, aliyense yemwe M'bale Branham anamupempherera, abwere kuno, ine ndikufuna kuti inu mupereke yankho kwa boma la United States, ndi kalata. Ndipo izo zikanakhala kuulutsa kwa ku dziko lonse konse. Ine ndikulingalira, mwinamwake anthu foro kapena faifi milioni akanayankhira ku kuitana uko ngati zikanadziwika. Mwaona?

⁸⁸⁷ Ndipo anthu amenewo, kapena ena a iwo anali atafa kale, atagonekedwa kwina ndi adokotala, n—ndi osamalira okufa. Ena a iwo anali ataphedwa mu ngozi; ena a iwo anafa imfa yachirengedwe. Ena a iwo anali atachita khungu, osamva, olumala, opiringizika, osautsika, amisala...ali mu zipatala, sanali kudziwa nkomwe kuti ife tinali mu chipatala tikuwapempherera iwo. Kuwabweretsa iwo, ankachita kuwatenga iwo. Iwo anali akumenyera mu njira yonse ndi kuzidula okha zidutswa, asakudziwa ngakhale komwe iwo anali. Mu maminiti asanu, nkukhala ali bwino, okoma, anthu okonda, ndi amalinaliro abwino masiku awo ena onse. Mukuona?

⁸⁸⁸ Ndizo...Ndi chiani izo? Si M'bale Branham. Ndi Yesu Khristu, Iye anandituma ine kuti ndiziwapempherera odwala. Tsopano pano pali chomwe chiri. Izo zizinakhale zochita bwino kwambiri mu Jeffersonville, pakuti, chifukwa chake ndi ichi. Tsopano, ine ndikufuna kuti inu mudziwe ine ndiri nawo amzanga ena a apafupi kwambiri ndi opambana omwe ali komwe kuno mu mzinda uno. Ngakhale mzinda iwoweni, boma la mzindawu, ine sindimalikonda ilo. Ine sindimakonda momwe uliri, ndipo sindinateropo konse; pamene ine ndinali mnyamata wamng'ono, nditakhala, ndikuwerenga mabuku anga a mbiriyakale, ine ndinkati, “Tsiku lina ine ndidzachokako kuno.” Mukuona?

⁸⁸⁹ Ine sindimakukonda ku Jeffersonville, kuno ndi ku chithaphwi, ndi kumusi kuno. Ndi kwa lowe kwenikweni, n—ndipo ndi koipa kwambiri. Mudzakwere pamwamba apo pa Spickert Knobs kapena kwinkawake, ndi kudzayang'ana pansa

chaku New Albany ndi Jeffersonville, ngati inu mukufuna kuti mudzawone. Taonani kuno, madokotala ngakhaleenso akunena tsopano, kuti, “Anthu a mchigwa chino akukhala osowa magari chifukwa cha momwe kuliri.”

⁸⁹⁰ Dona wamng’ono kumtunda kuno, Akazi a Morgan, anachiritsidwa ku khansa, anamutengera garu wawo ku chipatala uko, ankaganiza kuti iye anali ndi chiwewe. Inu mukudziwa chomwe izo zinali? Kukhazikika kwa zoipa ndi zinthu pa maudzu komwe iye amadutsako. Ndi malo osakhala awukhondo kwambiri.

⁸⁹¹ Wina anali mu Ankhondo, anapita uko ndipo anakatenga . . . Iye anali ndi mphumu. Anapita kumusi uku mu Florida ndipo maso ake anakhala okuda kwenikweni, ndipo anapita kwa adotolo, ndipo iye anati, “Adotolo . . .”

⁸⁹² Adotolo anati, “Tsopano, inu mwakhala muli kumenyana, sichoncho inu?”

⁸⁹³ Iye anati, “Ayi, bwana, ine sindinali.”

⁸⁹⁴ Ngati inu mukufuna kuti mudziwe yemwe iye ali, dzina lake ndi Herby. Tsopano, ngati ine nditatu ndingoganiza . . . N—ndi uku ku Union National Bank, mu New Albany, iye ndi kashiya. Mudzangopita uko ndi kukamuwona uyo wotchedwa “Herby,” mukamufunse iye.

⁸⁹⁵ Ndipo iye anati . . . Iye anapita, iye anati, “Adotolo,” iye anati, “ine ndiri ndi chimfine.”

⁸⁹⁶ Ndipo iye anamupima iye, anati, “Uko nkulondola.” Iye anati, “Ine ndimaganiza kuti iwe unali ukumenyana.” Anati, “Mnyamata, kodi iwe umakhala kuti?”

⁸⁹⁷ Iye anati, “Inu tsopano mukhoza kuwadziwa malowo,” anati, “Ine ndimakhala mu mzinda waung’ono patsidya pa Louisville, Kentucky, wotchedwa New Albany, Indiana.”

⁸⁹⁸ Anati, “Iwe ukutanthauza kundiuza ine kuti iwe watenga vuto la chimfine kuchokera mu madzi a mchere awa kuno mu Miami, ochokera?” Anati, “Ngati iwe ungakhoze kumakhala mu Jeffersonville, Indiana, kapena New Albany, Indiana, iwe ukhoza kukakhala kulikonse mu dziko lomwe ankhondo a United States angakutumize iwe.” Ndizo zonse. Mukuona?

⁸⁹⁹ Ndi malo opanda ukhondo kwambiri omwe alipo mu dziko, omwe ine ndikuwadziwa, kupatula kukanakhala ku chithaphwi china cha malungo. Mwaona? Ndipo i—i—i—ine ndiri nawo abwenzi kuno.

⁹⁰⁰ Penyani kuno, ine ndikhoza kupita kukawaitana iwo monga chonchi. Tayang’anani pa Dr. Sam Adair, bwanawe wanga. Chabwino, pali Mike Egan, wakhala apoyo. O, mai, ndi angati omwe ine ndikanawatchula! Basi mazana a mabwanawe abwino enieni, amzanga akale, omwe ine ndadziwana nawo . . . Ziribe kanthu abwenzi angati atsopano omwe ndimawapeza, palibe

chirichonse chingatenge malo a mzanga wakale. Inu mukudziwa zimenezo.

901 Apo pali amayi anga okalamba akhala mmbuyomo apo, alibe masiku ochuluka pa dziko lapansi, iwo ali mu zaka zao za sikisite tsopano. Apo pali amayi a mkazi wanga, sevente, akupita mu sevente-wani; akhala kumbuyo uko penapake, ine ndikuganiza, usikuuno. Ndipo apo, nkuwasiya iwo. Bambo anga anaikidwa komwe kuno; mkazanga anaikidwa kuno ku Walnut Ridge; mwana wanga wagona uko komwe. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

902 I—i—ine sindikukonda...I—i—ine sindikufuna kuti ndizikhala kuno, ndipo ine ndikukhulupirira kuti posachedwa, pompano, ine ndiyenera kuti ndichokeko. Mwaona, chifukwa izo zakhala zikubwera kwa ine, ine ndikuzinena izi paguwa apa ndiri ndi Baibulo langa, mowirikiza.

903 Pamene ine ndinamuza mkazi wanga, pamene iwo anatipatsa ife ndalama kuti timangire nyumba ya ubusa ija yomwe ine ndinaipereka kwa mpingo uno...Mpingo uno ndiwo mwini wa nyumba imeneyo; pitani kumusi uko, mukafufuze ngati izo siziri. Mwaona, ine sindikanati nditengere kwa inemwini.

904 Tsopano, pamene ine ndikapita kuti ndikaimange uko, Meda anati, “Ine ndikufuna kuti ndizikhala kuno pa chifukwa cha amayi anga.”

905 Ine ndinati, “Wokonedwa, motsimikiza basi monga ife tikuchitira, ife tidzakhala achisoni nazo. Mwaona, izo sizingagwire ntchito basi. Mulungu anati, ‘Dzipatule,’ ine ndiyenera kuti ndichite izo.”

906 Ndipo anati, “Chabwino, mayi anga!”

907 Ine ndinati, “Mayi anga, nawonso. ‘Koma iye amene sadzawasiya ake omwe, ndi kunditsatira Ine, sali woyenera kuti azitchedwa Wanga.’ Ndipo izo nzoona.”

908 Tsikulina, posachedwapa, ine ndikumverera kuti ndiyenera kuti ndisamuke, uko ndi kupita kwina. Koma njira yake ndi iyi, misonkhano siigwira ntchito kuno. Siigwira ntchito monga iyo imachitira kwina kulikonse, ndipo aliyense yemwe anayamba wakhalapo mu msonkhano akudziwa kuti izo nzoona, chifukwa ndi komwe kuno mu mzinda wanga womwe. Ndi zomwe ziri.

909 Yesu ananena chinthu chomwecho pamene Iye anabwera.

910 Iwo anati, “Kodi mnyamata uyu ndi ndani? Kodi uyo si mnyamata wa akalipentala a kunowa? Ndi sukulu iti yomwe iye anayamba wapitako? Kodi anakakutenga kuti kuphunzira kwakeko? Tsopano ndirole ine ndikuwone iwe ukuchita...Iwe unati umachita zozizwitsa tiye, ndirole ine ndikuwone iwe ukuchita chinthu chomwecho kuno. Zomwe iwe umachita mu Kaparenao, ndirole ine ndiwone iwe ukuzichita izo kuno.”

⁹¹¹ Yesu anati. . . “Iye anazizwa pa kusakhulupirira kwawo.” Iye anatembenuka ndipo anati, “Indetu, indetu, ine ndikuti kwa inu, mneneri samakhala ndi mphoto ngati iye akhala ali pakati pa anthu ake omwe ku mudzi wake womwe.” Ndi kulondola uko?

⁹¹² Ndipo ife tikudziwa. . . tayang’anani pa. . . Tamutengani Finney, tamutengani Sankey, Moody; tamutengani John Wesile, sakanakhoza konse kupita nazo izo, mwaona, mpaka iye atachoka ku dziko la kwawo. Tayang’anani pa—tayang’anani p—p—pa Moody. Pamene Moody, wosoka nsapato waku Boston, sakanakhoza kupita nazo nkomwe, iye anabwera ku Chicago iye asanakhale wotchuka. Mukuona? Iye anayenera kuzichotsa izo kwa ake omwe. Inu nthawizonse muziyenera kuti muzichita izo.

⁹¹³ Koma tsopano, kuno, Mulungu ayankha pemphero ngati inu muti muiwale kuti ndi William Branham; mwaona, ngati muti muiwale kuti ndi William Branham yemwe ali ndi chochita chirichonse nazo, ndi yemwe akuima kokha ndi kukupemphererani inu. Ndi Yesu Khristu yemwe anachita kale zomwe inu mwamupempha kuti achite, ngati inu mutangokhulupirira izo. Mukuona? Izo si chirichonse choti nkuchita. . . Ine ndiribe kanthu kochita ndi izo, kungoti ndikhale mboni. Koma zikuwoneka kuti poleredwera kuno limodzi ndi inu, ndipo inu mukudziwa chifooko chirichonse chomwe ine ndiri nacho, ndi kulakwitsa kulikonse komwe ine ndiri nako. . . Ndipo inu mukudziwa zomwe Mulungu wazichita, mu mzinda uno momwe.

⁹¹⁴ Mzinda uno, pa Tsiku la Chiweruzo, udzayankhira ndi mtengo wawukulu tsiku lina, pakuti pakhala pali mazana ndi mazana a machiritso odziwika komwe kuno. Ndiko kulondola, komwe kuno. Zizindikiro ndi zodabwitsa, ndi kuwonekera kwa Mngelo kumusi uko, ndi mapepala atalengeza uko ndi chirichonse. Ndipo komabe anthu sali. . . Nchifukwa chiani ziri chomwecho?

⁹¹⁵ Tsopano, tsiku lina, ine ndidzachokako kuno. Ine ndikudabwa, “Kodi mathero anga adzakhala otani?” Kodi izi zatha? Kodi izi zangotsala pang’ono? Ine ndiri usinkhu wa zaka forte eyiti. Kodi izi zangotsala pafupi kutha? Ine ndikudabwa izi, ngati ziri choncho.

⁹¹⁶ Taonani, chifukwa chiani dziko silinachizindikire chithunzi icho apo? Nchifukwa chiani iwo sanachigwire icho mofulumira kamene? Bwanji iwo sakuzigwira zinthu zina izi? Bwanji iwo sakuwagwira mauneneri awa ndi zinthu? Inu mukudziwa, iwo sangakhoze kuchita izo tsopano, koma tsiku lina ine ndidzachoka mdzikoli, ndipo pamene ine ndidzachoka, ndiye iwo adzazizindikira Izo. Ena a inu achinyamata mudzazizindikira izo ine nditapita kale. Mwaona? Koma Mulungu sakulola kuti izo zizichitidwa pano.



Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo, Bukhu Loyamba
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume One)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org